# Chibvomerezo cha London Baptist cha 1689

## Za mkatimu


1. Za Malemba Opatulika ........ 7
2. Za Mulungu ndi Utatu Woyera ........ 9
3. Za Zokhazikitsidwa ndi Mulungu ........ 11
4. Za Chilengedwe ........ 13
5. Za Momwe Mulungu Amasamalira Zolengedwa ........ 13
6. Za Kugwa kwa Munthu, Tchimo ndi Chilango Chake ........ 15
7. Za Chipangano cha Mulungu ........ 16
8. Za Khristu Mkhala Pakati ........ 17
9. Za Ufulu wa Chifuniro cha Munthu ........ 20
10. Za Kukwaniritsidwa kwa Kuitana ........ 21
11. Za Kuyesedwa Olungama ........ 22
12. Za Kukhala Mwana wa Mulungu ........ 23
13. Za Kuyeretsedwa ........ 24
14. Za Chikhulupiliro Chopulumutsa ........ 25
15. Za Kulapa Kotengera Munthu ku Moyo ndi Chipulumutso ........ 26
16. Za Zintchito za Bwino ........ 27
17. Za Kupilira kwa Anthu Oyera Mtima ........ 28
18. Za Chitsimikizo cha Chisomo ndi Chipulumutso ........ 30
19. Za Chilamulo cha Mulungu ........ 31
20. Za Uthenga wa Bwino, ndi za Mwezo wa Chisomo Chake ........ 33
21. Za Ufulu wa Chikhristu ndi Ufulu wa Chikumbumtima ........ 34
22. Za Chipembezo ndi Tsiku la Sabata ........ 35
23. Za Malumbiro Obvomerezeka ndi Kuwinda ........ 37
24. Za Udindo wa Boma ........ 38
25. Za Ukwati ........ 39
26. Za Mpingo ........ 40
27. Za Chiyanjano cha Okhulupilira ........ 43
28. Za Ubatizo ndi Mgonero wa Ambuye ........ 44
29. Za Ubatizo ........ 44
30. Za Mgonero wa Ambuye ........ 45
31. Za Kumwalira ndi Kuuka kwa Akufa ........ 47
32. Za Chiweruzo Chomaliza ........ 47

© Copyright 2016 Chapel Library, www.chapellibrary.org.

Permission is expressly granted to reproduce this material by any means, provided that 1) you do not charge beyond a nominal sum for cost of duplication, and 2) this copyright notice and all the text on this page are included.

Chapel Library sends Christ-centered materials from prior centuries worldwide without charge, relying entirely upon God's faithfulness. We therefore do not solicit donations, but we gratefully receive support from those who freely desire to give.

Please download material without charge from our website, or contact the international distributor as listed there for your country.

Mukafuna mabuku ena a Chikhristu, tilembereni kalata kapena kutiyimbira foni:

**Antioch Baptist Church**
PO Box 30610
Chichiri, Blantyre 3, Malawi
+265 998 470 177

*In Malawi, contact us for additional copies of this book or other Christ-centered materials. Subscriptions to the Free Grace Broadcaster are also available (in English).*

# Mbiri ya Chibvomerezo cha London Baptist cha 1689

M'zaka za 1630 ndi 1640 ku England anthu a m'mipingo yosiyanasiyana ndi a Baptist anatuluka mu mpingo waukulu wa ku England. Kukhala kwao kunali kovutika ndi zipsinjo zochokera ku nyumba ya malamulo ya mdzikomo ndi chipembedzo chomwe chinakhadzikitsidwa ndi mfumu wa ku England. M'ndandanda wa malamulo unakhadzikitsidwa kulanga aliyense wokana chipembedzo chokhadzikitsidwa ndi dziko limeneli. Zopsinja zimene zinadza ndi nthawi imeneyi chifukwa cha malamulowa zidatsatira kwambiri anthu a mipingo yoyima payokha, mipingo ya Presbyterian ndi mipingo ya Baptist.

A mpingo wa Presbyterian ndi mipingo yoyima payokha adavutuikanso chimodzimodzi ngati a mpingo wa Baptist chifukwa iwo adali ogwirizana mu ziphunzitso zawo. Ndipo kugwirizana kumeneku kunapangitsa kuti iwo akathe kutsutsana ndi malamulo a nkhaza ochokera ku boma. A Mpingo wa Presbyterian anakhadzikika pa chivomerezo cha chikhulupiro chawo cha Westminister cha mchaka cha 1658. Mipingo yoyima payokha inalandira mfundo za chikhulupiliro za mu Savoy Declaration ya mchaka cha 1658.

## Chibvomerezo cha chikhulupiliro cha Westminister cha mchaka 1647

M'mene nkhondo inabuka ku England pakati pa nyumba ya malamulo ya ma puritan ndi Mfumu (1642-1649), zinthu zina zinasitha mu mpingo wa Anglican. M'chaka cha 1643 ulamuliro wa ma bishop ku mpingo ndi dongosolo lake zinasinthidwa ndi nyumba ya malamulo. Ndondomeko ina inakhadzikitsidwa ndipo inali ndi anthu ogwira ntchito ya Mulungu okwanira zana limodzi ndi makumi awiri ndi m'modzi (121), ndi anthu wamba makumi atatu (30), ma membala a mnyumba ya House of Lords Khumi (10), ndi ma membela a House of commons makumi awiri (20). Msonkhano umenewu wa anthu aku Westminister umachitikira ku malo a mbiri a Westminister Abbey ku London ndipo ndi kumene dzina la chibvomerezo cha chikhulupiliro chawo linachokera.

Ambiri mwa anthu omwe anasonkhana nawo mchaka cha 1643 anali ma puritan a mpingo wa Presbyterian. Akulu akulu oyang'anira boma a ku Scotland okwana asanu ndi atatu analoledwa kukhala nawo pa msonkhanowu chifukwa iwo anatenga nawo gawo polimbana ndi mfumu

ya dziko la England. Ngakhale nthumwi za ku Scotland zinalibe udindo weni weni pa zokambiranazo, kukhala kwawobe kunali kothandiza. Msonkhanowu unali ndi magawo okwanira chikwi ndi zana limodzi ndi makumi asanu ndi khumi ndi atatu pakati pa mwezi wa July 1, 1643, ndi February 22, 1649.

Pamene ntchito inali kupitilira, ndondomeko ya Chipembezo inakonzedwa kuti ilowe m'malo mwa buku la mapemphero lomwe lidaikidwa ndi ma bishop. Kuphatikizira apo chibvomerezo cha chikhulupiliro cha tsopano chinalembedwa ku mpingo wa ku England. Chibvomerezo cha chikhulupiliro cha Westminister chakhala chofunikira kwambiri ku ntchito ya kukonzanso ya reformation. Ntchito yolemba chibvomerezochi inayamba mu July 1645 ndipo idapitilira ndi zobvuta zambiri mpakana kumalizika kwake mu December 1646. Chibvomerezochi chinabweretsedwa ku ma nyumba a Malamulo onse awiri mchaka cha 1647 pansi pa dzina loti "The humble advice of the assembly of Divines, Quotations and texts of scripture Annexed, Presented by Them lately to both Houses of Parliament."

*Chibvomerezo cha Westminister,* ndi chidule cha zikhulupiliro zikuluzikulu za chikhristu zokwana m'magawo makumi atatu ndi atatu. Ziphunzitso za baibulo ndi zomwe zili mchibvomerezochi, kutsindikiza za chipangano cha ubale wa pakati pa Mulungu ndi munthu. Pa kayendetsedwe ka mpingo chibvomerezochi chima gwirizana ndi mpingo wa Presbyterian ponena kuti mipingo ikuyenera kukhala pansi Msonkhano wa akulu akulu otchedwa (synod). Chibvomerezochi chimanena za ubatizo wa ana. Westminister imakhulupilira kuti Mulungu amapulumutsa banja lonse ndipo mwana wa khanda amatengedwa ngati m'modzi mwa amu chipangano kudzera mwa makolo ake pokha ataonetsera kuti iye siali m'mchipangano kudzera mu zochita zake.

Kuthandizira kufotokoza chibvomerezochi katekisimu wamkulu analembedwa ndi Msonkhano wa Westminister kuti azigwiritsidwa ntchito ndi azitumiki polalikira. Katekisimu wa ng'ono anapangidwira kuphunzitsa ana achichepere.

Ngakhale chibvomerezo cha Westminister sichinagwiritsidwe kwa nthawi yayitali ndi Mpingo wa ku England, msonkhano waukulu wa mpingo wa ku Scotland unagwiritsira ntchito chibvomerezochi kwa nthawi yayitali. Ngakhale lero lino chibvomerezochi chimagwiritsidwa mu mipingo ya Presbyterian yambiri.

## Savoy Declaration (1658)

A Khristu omwe samagwirizana ndi kusintha kwa zinthu mwa zizizi anapeza kuti chibvomerezo cha Westminister ndi choyanjana ndi Mawu a

Mulungu koma iwo sanagwirizane nawo pa kayendetsedwe ka mpingo ndi ubatizo wa ana a khanda. Ndi magulu amanewa anakhalapo awiri: Mpingo woyima pawokha (Congregationalists) ndi a Baptist.

Pofuna kupitilira ndi gulu lochuluka la anthu lomwe a Congregationalists anali nalo iwo anakumana ku Savoy Palace ku London pa September 29, 1658. Synod yawo inatengera lamulo la chikhulupiliro ndi ndondomeko, yolemekezeka ndi kutsatidwa mu mipingo yoyima payokha. Savoy declaration inatengera Westminister muzambiri komabe iwo anaonjezera za kukhadzikitsa kwa mipingo ndi kusankhidwa kwao ndi Yesu Khristu.

## Chibvomerezo cha London Baptist cha 1677

Amene anali omvetsetsa mawu a Mulungu pa za ubatizo wa anthu okhulupilira nawonso anafunikira chibvomerezo cha chikhulupiliro chawo. Awo amatchedwa ma Baptist. Pa ku vutikira limodzi ndi ma Presbyterian ndi ma Congragationalists nawonso a Baptist anasonkhana limodzi kuti alembe za chiphunzitso chawo.

Kunalembedwa chikalata kupita ku mipingo ya baptist yosiyanasiyana mdziko la England ndi Wales kuuza mipingoyi kuti itumize mthumwi ku msonkhano ku London mchaka cha 1677. Chibvomerezo chofanana ndi cha Westminister chinakhazikitsidwa. Kuyambira kale chinakhala chotchedwa London Baptist Confession ya 1677. Chifukwa chokuti chibvomerezochi chinakhazikitsidwa nthawi ya zipsinjo chinaperekedwa mwa chibisira.

Mawu otsogolera mu kulemba koyamba kwa 1677 anati “pakuti kwa nthawi yaitali ambiri mwa ife tinazindikira za kufunika kolemba chibvomerezo cha chikhulupiro chathu kuti tikathe kudziwitsa onse amene sanali kumvetsa mfundo zathu ndipo anali ndi malingaliro olakwika okhudzana ndi chipembezo chathu.”

“Tinachiona chofunikira kuti tikambe za chikhulupiliro chathu mwatchutchutchu, pakuti sitinapeze cholakwika chilichonse kupanga choncho ngati momwe anapangira anzathu a Westminister, ngakhalenso a Congregational. Tinachiona kuti ifenso tichite chimodzimodzi mu chibvomerezo cha chikhulupiliro chathuchi, osakamba zosiyana ndi anzathuwa, tagwiritsa ntchito mawu ofanana. Tinapanga izi kuti titsimikizire onse kuti tilibe cholinga chofuna kuyika mawu ena atsopano ku chipembezo koma kugwiritsa mawu amene anthu ena anagwiritsa ntchito kale. Mu zinthu zomwe tikusiyana maganizo ndi anthu ena izi tanena poyera, ndipo sitikufuna kuchita mikangano ndi konse.”

## Chibvomerezo cha London Baptist cha 1689

William ndi Mary anakhala pa mpando wa chifumu mchaka cha 1689. Pa May 24 chaka chomwecho mchitidwe wovomereza maganizo osiyana pa zinthu zochitika unakhazikitsidwa. Patangopita miyezi iwiri azibusa ochokera ku London anaitanitsa msonkhano waukulu wa anthu a Baptist kuchokera ku England ndi Wales. Mthumwi zochokera ku mipingo zana limodzi ndi asanu ndi awiri anakumana ku London pa September 3 mpakana pa September 12. Iwo anatenga chibvomerezo cha London Baptist cha 1677 ndi kukonza zinthu zina zofunikira.

Chinthu chimodzi chomwe chinapangitsa mpingo wa Baptist kuti ukule ndi kusiyana kwao ndi anthu ena. Ma Baptist sanali kugwiritsa ntchito ma sacrament ngati a Mpingo wa Anglican kapena a chikatolika amachitira. Iwo amakhulupilira malamulo awiri: Mgonero wa Ambuye ndi ubatizo wa anthu okhululupilira. A mpingo wa Baptist oyambirira amakhulupilira kubatizidwa pa kuviikidwa m'madzi amene anali kuyenda, amu mtsinje kapena khwawa. Kayendetsedwe ka mpingo kanali kokuti mpingo ndi umene uyenera kuzilamulira, unali ndi mphamvu zoyitana mtumiki kapena kumuchotsa. Kunalibe ma bishop kapena oyang'anira mu ndondomeko ya Baptist, panalibe mpingo womwe unali ndi mphamvu pa mpingo unzake.

Mwachidule, kumvetsetsa kwa chikhulupiliro cha chikhristu momwe Baibulo limanenera kunalembedwa mu chibvomerezo cha Westminister cha 1647. Zokonzanso zinachitidwira 1) mpingo wa anthu oyima paokha wa Congregationalists mu Savoy Declaration ya 1658, 2) ubatizo wa anthu okhulupilira mu Chibvomerezo cha London Baptist cha 1677.

Thunthu la chibvomerezo cha westminister linabwerezedwa mu chibvomerezo cha London Baptist cha 1689, chomwenso chinaphatikizanso zina mwa zomwe zinali mu Savoy Declaration ndi chibvomerezo choyambilira cha London Baptist. Chibvomerezo ichi cha London Baptist chakhala cha mngwiro kwa nthawi yaitali ndipo chakhala chimodzi mwa zofunikira mu zofotokoza za chikhulupiliro cha chikhristu mu mbiri ya Mpingo. Mipingo yambiri pa dziko lapansi imagwiritsa ntchito chibvomerezochi.

# Mutu 1
# Za Malemba Opatulika

**1** Malemba Opatulika ndi njira[a] yokhayo yotitengera ku chidziwitso, chikhulupiliro cha chipulumutso, ndi kumvera kwa chipulumutso yomwe ili yokwanira, yotsimikizizika komanso yopanda cholakwika, ngakhale chilengedwe[b] komanso ntchito ya kulenga ndi chisamaliro cha Mulungu pa zolengedwa Zake zimatiwonetsera ubwino, nzeru ndi mphamvu ya Mulungu kotero kuti munthu alibe ponamizira; komabe chilengedwe pachokha sichipereka mokwanira chidziwitso cha Mulungu ndi chifuniro Chake zofunikira pa chipulumutso cha munthu. Kotero kunamkondweretsa Mulungu ku nthawi zosiyanasiyana ndi munjira zosiyanasiyana[c] kuti akazidziwitse Yekha ndi kuonetsera chifuniro chake kwa mpingo wake; ndipo potsatira izi kuti choonadi chisungike ndi kufalitsidwa, komanso kuti mpingo ukhazikike potetezedwa ku chiononongeko cha zolakwika zathupi, umbanda wa Satana ndi wa dziko lapansi ndi kuika izi m'malemba[d]; zomwe zikuchititsa kuti Malemba opatulika akhale ofunikira. Njira za Mulungu zakale zoonetsera chifuniro Chake kwa anthu ake zinatha.

([a]2 Timoteo 3:15-17; Yesaya 8:20; Luka 16:29, 31; Aefeso 2:20; [b]Aroma 1:19-21; 2:14-15; Masalimo 19:1-3; [c]Ahebri 1:1; [d]Miyambo 22:19-21; Aroma 15:4; 2 Petulo 1:19-20)

**2** Tsopano mabuku onse a mu chipangano cha kale ndi chatsopano ali pansi pa dzina loti Malemba Opatulika kapena Mawu a Mulungu, ndipo mabukuwo ndi awa:

**Chipangano Chakale**

Genesis, Eksodo, Levitiko, Numeri, Deuteronomo, Yoswa, Oweruza, Rute, 1 Samueli, 2 Samueli, 1 Mafumu, 2 Mafumu, 1 Mbiri, 2 Mbiri, Ezara, Nehemiya, Estere, Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki, Nyimbo, Yesaya, Yeremiya, Maliro, Ezekieli, Danieli, Hoseya, Yoweli, Amosi, Obadiya, Yona, Mika, Nahumu, Habakuku, Zefaniya, Hagai, Zekariya, Malaki

**Chipangano Chatsopano**

Mateyu, Marko, Luka, Yohane, Machitidwe, Aroma, 1 Akorinto, 2 Akorinto, Agalatiya, Aefeso, Afilipi, Akolose, 1 Atesalonika, 2 Atesalonika, 1 Timoteo, 2 Timoteo, Tito, Filemoni, Ahebri, Yakobo, 1 Petro, 2 Petro, 1, 2, 3 Yohane, Yuda, Chibvumbulutso

Onse amene adauziridwa[e] ndi Mulungu kuti akakhale olamulira mchikhulupiro chathu ndi moyo wathu. ([e]2 Timoteo 3:16)

**3** Mabuku otchedwa Apocrypha sanauziridwe[f] ndi Mulungu, ndipo siali mawu a Mulungu, ndipo alibe lamulo lililonse ku Mpingo komanso sakuyenera kuwonedwa mosiyana ndi zolemba zilizonse za anthu wamba.

([f]Luka 24:27, 44; Aroma 3:2)

**4** Ulamuliro wa Mawu Opatulika, umene tikuyenera kukhulupilira, sudalira umboni wochokera kwa munthu kapena mpingo, koma umadalira [g]Mulungu Yekha (amene ali choonadi Iye Yekha) amene ali mwini wolemba; choncho akuyenera kulandilidwa chifukwa ndi Mau a Mulungu.

([g]2 Petro 1:19-21; 2 Timoteo 3:16; 2 Atesalonika 2:13; 1 Yohane 5:9)

**5** Titha kusunthika ndi umboni wa mpingo kuti tilemekeze kwambiri Malemba Opatulika, ulemelero wawo, chiphunzitso chawo chosuntha moyo, komanso kalembedwe kawo, kugwirizana kwa magawo onse, thunthu lawo (lomwe limapereka ulemelero kwa Mulungu). Zonse zomwe malembawa amapeza pa za njira yokhayo ya chipulumutso cha munthu ndi zopambana zosafananizika, kupanda banga kwake ndi mfundo zomwe zimazichitira umboni kuti ndi Mawu a Mulungu. Komanso osaiwala kuti kukhutira kwathu ndi [h]chitsimikizo cha choonadi chopanda kuthekera kolakwika, ndi ulamuliro wake wa Umulungu, zili choncho chifukwa cha ntchito yomwe Mzimu Woyera amagwira mkati mwathu kuchitira umboni kudzera m'Mawu Opatulika.

([h]Yohane 16:13-14; 1 Akorinto 2:10-12; 1 Yohane 2:20, 27)

**6** Uphungu wonse wa Mulungu wokhudzana ndi zinthu [i]zoyenera ulemelero wake, chipulumutso cha munthu, chikhulupiliro ndi moyo, zimapezeka m'malemba opatulikawa, amene sakuyenera kuonjezeredwa kapena kuchotseredwa kudzera ku mabvumbulutso ena a Mzimu kapena zikhalidwe za anthu.

Ngakhale zili choncho, timavomerezabe za [k]kuwunikira kwa Mzimu mkati mwathu kukhala kofunikira pakupereka kuthekera komvetsetsa zinthu zomwe zinalembedwa M'malemba, ndipo pali zinthu zina zokhuzana kapembedzedwe ka Mulungu ndi kayendetsedwe ka Mpingo, zomwe zikuyenera [l]kulamulilidwa ndi kuwala kwa chilengedwe komanso nzeru za Chikhristu, malingana ndi malamulo a Mawu, omwe akuyenera kutsatidwa.

([i]2 Timoteo 3:15-17; Agalatiya 1:8-9; [k]Yohane 6:45;
[l]1 Akorinto 11:13-14; 14:26,40)

**7** Zinthu zonse M'malemba opatulika si zofanana [m]m'kamvetsetsedwe kawo ndipo sizomvetsetseka kwa anthu onse; komabe zinthu zomwe ndi zoyenera kuzidziwa, kudzikhulupilira kuti munthu akathe kupulumuka

zinalembedwa [n]momveka bwino m'malo osiyanasiyana m'malemba kuti onse ophunzira kapena osaphunzira athe kumvetsetsa mokwanira.

([m]2 Petro 3:16; [n]Masalimo 19:7; 119:130)

**8** Chipangano Chakale chinalembedwa mu chiyankhulo chomwe anthu a kale a Mulungu amayankhula, [o]chi Hebri, ndipo Chipangano Chatsopano chinalembedwa mu chi Helene, (chifukwa pa nthawi imene kumalembedwa chipanganochi maiko ambiri amayankhula chiyankhulochi). Mawuwa anauziridwa ndi Mulungu, ndi mwachisamaliro chake anawasunga oyera mzaka zonse ndipo ali [p]obvomerezeka; chifukwa cha ichi pa nkhani zonse za chipembezo mpingo wa Yesu ukuyenera kumvera Mawuwa.

Koma chifukwa chokuti [q]ziyankhulo zomwe Baibulo linalembedwera sizimadziwika ndi anthu onse a Mulungu, omwe ali ndi ufulu odziwa komanso chikhumbokhumbo chofuna mawu a Mulungu, ndipo akulamulidwa kuti ndi mtima woopa Mulungu [r]adziawerenga ndi kuwafufuza mawuwa, akuyenera kumasuliridwa mu ziyankhulo zonse za pa dziko lirilonse lomwe [s]litafikiridwe ndi mauwa, ndi cholinga choti mawu a Mulungu akakhala [t]ochuruka mwa onse, akathe kumupembedza Iye moyenera, ndi kupeza mtendere ndi chiyembekezo m'Malemba Oyera.

([o]Aroma 3:2; [p]Yesaya 8:20; [q]Machitidwe 15:15; [r]Yohane 5:39; [s]1 Akorinto 14:6,9,11-12,24,28; [t]Akolose 3:16)

**9** Potanthauzira Malemba tikuyenera kugwiritsa ntchito [u]Malemba omwewo; ndipo ngati pali malemba ena omwe sali kumvetsetseka tikuyenera kuwerenga malo ena amene angalongosole momveka bwino.

([u]2 Petro 1:20-21; Machitidwe 15:15-16)

**10** Malemba ndiye oweruza wamkulu wa mikangano yonse yokhudzana ndi zipembezo, maganizo a anthu olemba a kale kale, ziphunzitso za anthu, mizimu yosiyana siyana, zonsezi zikuyenera kuyesedwa ndi Malemba, komanso ife tonse tikuyenera kutsamira pa Malemba okhawo amene anaperekedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo mwa [x]Malemba chikhulupiro chathu chimalimbikitsidwa.

([x]Mateyu 22:29, 31-32; Aefeso 2:20; Machitidwe 28:23)

## Mutu 2

# Za Mulungu ndi Utatu Woyera

**1** Mulungu wathu ndi m'modzi[a] wamoyo ndi woonadi; amene[b] chilichonse chake chili mwa Iye yekha, [c]wopanda malire, wopanda banga

lililonse, amene ukulu wake palibe angaumvetse kupatula Iye mwini, [d]Mzimu wa kuyera konse, [e]wosaoneka ndi maso, wopanda thupi, chiwalo, zokhumba, yemwe ali ndi muyaya, wokhala mu kuunika koti munthu sangathe kufikira, [f]amene samasintha, [g]wamkulu kwambiri, [h]wosatha, wosamvetsetseka, [i]wamphamvu zonse, wopanda malire mu njira zonse, [k]wopatulika, wa nzeru zonse, womasuka, wotsimikizika, [l]wopanga chinthu chinachilichonse malingana ndi uphungu wa chifuniro chake choyera konse ndi chimene sichimasintha [m]chifukwa cha ulemerero wake; wachikondi chonse, wachisomo, chifundo, wopilira, wodzadza ndi ubwino ndi chilungamo, wokhulukira machimo, zolakwitsa zathu, [n]wobwezera mphoto kwa iwo omfuna Iye, Iye ndi wachilungamo ndi [o]wooMasalmo mu maweruzo ake onse, [p]kudana ndi tchimo ndi amene sadzalora kuti [q]wolakwa akhale osaweruzidwa.

([a]1 Akorinto 8:4,6; Deuteronomo 6:4; [b]Yeremiya 10:10; Yesaya 48:12; [c]Eksodo 3:14; [d]Yohane 4:24; [e]1 Timoteo 1:17; Deuteronomo 4:15-16; [f]Malaki 3:6; [g]1 Mafumu 8:27; Yeremiya 23:23; [h]Masalmo 90:2; [i]Genesis 17:1; [k]Yesaya 6:3; [l]Masalmo 115:3; Yesaya 46:10; [m]Miyambo 16:4; Aroma 11:36; [n]Eksodo 34:6-7; Ahebri 11:6; [o]Nehemiya 9:32-33; [p]Masalmo 5:5-6; [q]Eksodo 34:7; Nahumu 1:2-3)

**2** Mulungu wokhala ndi [r]moyo wonse, [s]ulemelero wonse, [t]ubwino, odala, mwa Iye yekha, ali Yekha wokwanira zonse, [u]wopanda kufuna chithandizo kwa zolengedwa zake, salandira ulemelero kuchokera kwa zolengedwa zake koma Iye amaonetsera ulemelero wake, kudzera pa iwo ndi kwa iwo; Iye ndi yekha gwero la umoyo wonse, [x]amene kudzera mwa Iye ndi kwa Iye kuli zinthu zonse ndipo ali ndi [y]ulamuliro ndi ukulu pa zolengedwa zonse, kuchita kudzera kwa iwo, kuchitira iwo, ndi pa iwo chilichonse chomwe chamukondweretsa; [z]pamaso pake palibe chinthu chobisika, nzeru zake ndi zopanda [a]malire ndi zopanda kulakwika kwinakulikonse ndipo sizimadalira zomwe [b]adazilenga, ndipo kwa Iye chilichonse palibe chosatsimikizika ndi kusaziwika; ali wopatulika mu uphungu wake wonse, zintchito zake zonse ndi malamulo ake onse; kwa Iye ulemelero, matamando, kumvera, kutumikira, kuchokera kwa [c]angelo ndi anthu onse kukuyenera kupatsidwa nthawi zonse.

([r]Yohane 5:26; [s]Masalmo 148:13; [t]Masalmo 119:68; [u]Yobu 22:2-3; [x]Aroma 11:34-36; [y]Daniele 4:25,34-35; [z]Ahebri 4:13; [a]Ezekiele 11:5; Machitidwe 15:18; [b]Masalmo 145:17; [c]Chivumbulutso 5:12-14)

**3** Mu Umulungu Wake ndi kukhala kopanda malire kwake, alipo makhalidwe atatu, [d]Atate, Mau kapena Mwana, ndi Mzimu Woyera, akukhala chimodzimodzi, mu mphamvu, muyaya, aliyense ali Mulungu koma [e]osagawikana; Atate ali osalengedwa, osabelekedwa, osachokera kwa

wina; Mwana [f]kunthawi zosatha Iye anali ndi Atate, ndi kukhazikika mu umodzi ndi Atate, Mzimu [g]akuchokera kwa Atate ndi Mwana, wonse ndi wopanda malire, wopanda chiyambi, kotero wonse ndi Mulungu m'modzi. Wopanda kusiyana mchikhalidwe chake, koma kusiyana kulipo pa ntchito ndi udindo omwe ulipo pa ubale wawo; Chiphunzitso cha Utatu Woyera ndi maziko a ubale wathu ndi kukhala kwathu pamodzi ndi Mulungu ndi kukhala wodalira Iye.

([d]1 Yohane 5:7; Mateyu 28:19; 2 Akorinto 13:14; [e]Eksodo 3:14; Yohane 14:11; 1 Akorinto 8:6; [f]Yohane 1:14,18; [g]Yohane 15:26; Agalatiya 4:6)

## Mutu 3

# Za Zokhazikitsidwa ndi Mulungu

**1** Mulungu [a]anakhazikitsa mwa Iye yekha kuyambira kunthawi yosatha, molingana ndi nzeru zake, uphungu wake, chifuniro chake, mopanda womuletsa ndi mopanda kusintha kulikonse, zinthu zonse, chilichonse chomwe chimachitika; Koma tikuyenera kudziwa kuti Mulungu si amene anayambitsa [b]uchimo kapenanso kuti ali ndi ubale uliwonse ndi tchimo. Chifuniro cha munthu sichikakamizidwa kuchita zoipa, komanso zotsatira za zintchito za anthu sidzichotsedwa koma [c]zimakhazikitsidwa, kudzera mwa izi timaona nzeru zake pakugwiritsa ntchito zinthu zonse, ndi mphamvu zonse ndi kukhulupilika[d] kwake pa kukwaniritsa zomwe anakhazikitsa kale.

([a]Yesaya 46:10; Aefeso 1:11; Ahebri 6:17; Aroma 9:15,18; [b]Yakobo 1:13; 1 Yohane 1:5; [c]Machitidwe 4:27-28; Yohane 19:11; [d]Numeri 23:19; Aefeso 1:3-5)

**2** Ngakhale Mulungu amadziwa chilichonse chomwe chitachitike pa nthawi yake[e] ndi momwe zichitikire, Iye anakhazikitsa zonse ndi kukonzeratu zonsezi[f], osati chifukwa choti Iye anazidziwiratu kuti zidzachitika motero mtsogolo ayi.

([e]Machitidwe 15:18; [f]Aroma 9:11,13,16,18)

**3** Kudzera mu kulamulira kwa Mulungu, poonetsera ulemelero Wake, anthu ndi angelo[g] ena adakonzedwera kukhala ndi moyo wosatha kudzera mwa Yesu Khristu, kuti chisomo chake chikatamandidwe[h]; pamene ena anasiyidwa ku machimo awo kuti akalandire chigamulo chawo[i], kuti chilungamo chake cha Mulungu chikaonekere ndi kutamandidwa.

([g]1 Timoteo 5:21; Mateyu 25:34; [h]Aefeso 1:5-6; [i]Aroma 9:22-23; Yuda 4)

**4** Angelo ndi anthu amenewa amene adalembedwa maina awo kale, ndipo sangasinthe konse, chiwerengero[k] chawo sichingaonjezeredwe kapena kuchotseredwa.

(2 Timoteo 2:19; Yohane 13:18)

**5** Kwa anthu[l] omwe anakonzedwera ku moyo, Mulungu, asanalenge dzikoli, molingana ndi cholinga chake cha muyaya ndi chosasintha ndi chinsinsi cha uphungu wake, ndi chifuniro chake, anasankha iwo mwa Yesu ku ulemelero wa muyaya mwa chisomo chake chaulere ndi chikondi chake, popanda chifukwa chilichonse mwa munthuyo[m] kuti Mulungu akathe kumusankha.

([l]Aefeso 1:4,9,11; Aroma 8:30; 2 Timoteo 1:9; 1 Atesalonika 5:9; [m]Aroma 9:13,16; Aefeso 2:5,12)

**6** Pakuti Mulungu anasankha anthu ena ku ulemelero wake, Iyenso mwa chifuniro chake anakonza njira[n] yomwe amene ali osankhidwa, komanso ochimwa mwa Adamu [o]adzawomboledwe ndi Khristu, adzaitanidwe[p] kuti akakhulupire mwa Yesu ndi Mzimu Woyera mu nthawi yoyenera, adzalungamitsidwe, ndi kupatsidwa umwana wa Mulungu, kupatulidwa ndi kusungidwa kudzera mu mphamvu Yake mwa chikhulupiliro ku chipulumutso[q]. Palibenso ena amene amawomboledwa ndi Khristu, kapena kuyitanidwa, kulungamitsidwa, kupatsidwa umwana wa Mulungu, kupatulidwa ndi kupulumutsidwa kupatula anthu osankhidwa okha[r].

([n]1 Petro 1:2; 2 Atesalonika 2:13; [o]1 Atesalonika 5:9-10; [p]Aroma 8:30; 2 Atesalonika 2:13; [q]1 Petro 1:5; [r]Yohane 10:26, 17:9, 6:64)

**7** Chiphunzitso chimenechi chodabwitsa cha kukonzedweratu kwa zinthu chikuyenera kutengedwa mosamalitsa, kuti amene afufuza za chifuniro cha Mulungu cholembedwa m'mawu Ake, ndikumvera mawuwo kuchokera pa kutsimikizika kwa ntchito yawo, akakhale otsimikiza mumtima za kuitanidwa ndi kusankhidwa[s] kwao ku nthawi ya muyaya. Kotero chiphunzitsochi chikuyenera kuchititsa munthu kuti ayamike[t], alemekeze, komanso akuze Mulungu, ndi kuchititsa munthu kukhala odzichepetsa[u], wa changu ndi kupereka chitonthozo chochuluka[x] kwa onse amene amakonda ndi kumvera Uthenga Wabwino.

([s]1 Atesalonika 1:4-5; 2 Petro 1:10; [t]Aefeso 1:6; Aroma 11:33; [u]Aroma 11:5,6,20; [x]Luka 10:20)

# Mutu 4
# Za Chilengedwe

**1** Pachiyambi zinamkondweretsa Mulungu Tate, Mulungu [a]Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera, kuonetsera [b]mphamvu Yake, nzeru zake, ndi ubwino wake polenga dzikoli ndi zonse za mkati mwake, [c]zooneka ndi maso ndi zonse zosaoneka ndi maso, kwa masiku asanu ndi limodzi ndipo zonse zinali bwino.

([a]Yohane 1:2-3; Aheberi 1:2; Yobu 26:13;
[b]Aroma 1:20; [c]Akolose 1:16; Genesis 1:31)

**2** Mulungu atatha kulenga zolengedwa zina zonse, Iye adalenga Munthu, [d]mwamuna ndi mkazi, anawalenga [c]mchiyero ndi mizimu yosafa, kuwapangitsa kukatha kukhala moyo womwe Mulungu anawalengera; anapangidwa [f]mchifaniziro Chake mu mzeru, chiyero, ndi kupatulika; okhala ndi lamulo la Mulungu [g]lolembedwa m'mitima yawo, ndi kuthekera kokwaniritsa lamuloli, komanso ndi kuthekera kolakwitsa pamene atasiyidwa mu ufulu wa chifuniro chawo womwe unali ndi [h]kuthekera kosintha.

([d]Genesis 1:27; [c]Genesis 2:7; [f]Mlaliki 7:29; Genesis 1:26;
[g]Aroma 2:14-15; [h]Genesis 3:6)

**3** Ngakhale lamulo linalembedwa m'mitima yawo, [i]anapatsidwa lamulo lakuti asadye za mu mtengo wakudziwitsa chabwino ndi choyipa. Iwo adali kukhala mokondwa pamene anali kusunga lamuloli, anali kukondwera pokhala pamodzi ndi Mulungu, ndipo anali ndi [k]ulamuliro pa zolengedwa zonse.

([i]Genesis 2:17; [k]Genesis 1:26-28).

# Mutu 5
# Za Momwe Mulungu Amasamalira Zolengedwa

**1** Mulungu Mlengi wabwino wa zonse, mu mphamvu zake zopanda malire ndi nzeru zake amanyamula[a], amalamulira komanso kuyendetsa zolengedwa zake zonse, zazikulu ndi zazing'ono[b] zomwe ndi nzeru zake komanso chisamaliro chake chopatulika kucholinga chomwe izo zinalengedwera, molingana ndi momwe Iye adadziwira kale ndi uphungu

wa chifuniro chake umene sumasintha nthawi zonse[c] kuti akalemekezeke mu nzeru zake, mphamvu, chilungamo, ubwino wake wopanda malire, ndi chifundo.

([a]Ahebri 1:3; Yobu 38:11; Yesaya 46:10-11; Masalimo 135:6; [b]Mateyu 10:29-31; [c]Aefeso 1:11)

**2** Ngakhale zili molingana ndi kudziwiratu ndi kukhazikitsiratu kwa zinthu kwa Mulungu, zinthu zonse zimachitika[d] popanda kusintha kulikonse kapena kulakwika kulikonse; kotero kuti palibe chinthu chomwe chimachitika mwa ngozi[e] kapena popanda chisamaliro chake, ngakhalebe kudzera mu chisamaliro chomwechi anakonza kuti zinthu zikachitike pogwiritsa ntchito zapansi pano; kaya mwa kufunikira[f] kapena motengera zochitika zina.

([d]Machitidwe 2:23; [e]Miyambo 16:33; [f]Genesis 8:22)

**3** Mulungu mwa chisamaliro[g] chake amagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana, ngakhale Iye ali ndi ufulu[h] wochita zinthu popanda[i] njirazi, kapena mosiyana[k] ndi njirazi momwe Iye wasangalatsidwira.

([g]Machitidwe 27:31,44; Yesaya 55:10-11; [h]Hoseya 1:7; [i]Aroma 4:19-21; [k]Danieli 3:27)

**4** Mphamvu zonse, nzeru zosafufuzika, ndi ubwino wopanda malire wa Mulungu, zimaonetseredwa mu chisamaliro chake kuti uphungu wake[l] umafikira ngakhale kugwa kwa Munthu pachiyambi mpakana zochimwa zina za angelo ndi anthu; zimenezi sizichitika mwa chilolezo chake chabe chimene Iye amathanso kupereka mwa nzeru zake komanso mphamvu[m] zake, Iye amalamulira kuti zinthu zichitike kuti chifuniro chake chopatulika chikachitike[n]; koma ngakhale zili chonchi uchimo wa anthu umachokera mwa anthu eniake osati Mulungu, amene ali woyera koposa komanso wa chilungamo, ndiponso Iye sangathe kuyambitsa kapena kubvomereza[o] tchimo.

([l]Aroma 11:32-34; 2 Samueli 24:1; 1Mbiri 21:1; [m]2 Mafumu 19:28; Masalimo 76:10; [n]Genesis 50:20; Yesaya 10:6-7,12; [o]Masalimo 1:21; 1 Yohane 2:16)

**5** Mulungu wa nzeru zonse, wachiyero ndi wachisomo, kwa nthawi ndi nthawi amawasiya ana ake ku mayesero osiyanasiyana ndi kuzoonongeka za m'mitima yawo, kuti akathe kuwalanga iwo chifukwa cha machimo awo a m'mbuyo, kapena kuwazindikiritsa iwo mphamvu ya zinthu zolakwika zomwe zili m'mitima[p] yawo, kuti iwo achepetsedwe ndi kuti adzifuna kuyenda ndi Mulungu pafupi ndi kumudalira Iye pa chilichonse chokhudzana ndi moyo wawo; komanso kuwapangitsa iwo kukhala osamalitsa pa kuthekera kulikonse kochimwira Mulungu, komanso

zolinga zina za Mulugu. Choncho pa chilichonse chomwe chimamuchitikira munthu wosankhidwa ndi Mulungu, zimakhala malingana ndi momwe Iye anakonzera, kuti akalandire ulemelero ndikutinso zikachitire ubwino[q] anthu ake.

([p]2 Mbiri 32:25-26,31; 2 Akorinto 12:7-9; [q]Aroma 8:28)

**6** Anthu onse ochimwa ndi osatembenuka mtima amene Mulungu monga Oweruza woyera, chifukwa cha zochimwa zawo amawapatsa khungu[r] ndi kuumitsa mitima yawo, kwa oterewa samapereka chisomo[s] chake, pakuti akanalandira chisomo chake akanatha kuzindikira komanso mitima yawo ikanakhudzidwa; ndiponso nthawi zinanso amawalanda mphatso[t] zomwe adali nazo ndi kuwasiya kuzinthu[u] za kuonengeka ndi uchimo, ndi kuwasiya ku zilakolako zawo[x], ku mayesero a m'dzikoli ndi ku mphamvu za Satana, ndipo zimachitika kuti amaumitsa mitima yawo pogwiritsa njira zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito kufewetsera mitima ya anthu ena.

([r]Aroma 1:24-26,28; 11:7-8; [s]Deuteronomo 29:4; [t]Mateyu 13:12;
[u]Deuteronomo 2:30; 2 Mafumu 8:12-13; [x]Masalimo 81:11-12;
2 Atesalonika 2:10-12; [y]Eksodo 8:15,32; Yesaya 6:9-10; 1 Petro 2:7-8)

**7** Monga momwe chisamaliro cha Mulungu chimafikira zolengedwa zake zonse, mwa njira yapadera amasamalira Mpingo wake[z] ndipo amagwiritsa ntchito zinthu zonse kuti zichitire ubwino iwo.

([z]1 Timoteo 4:10; Amosi 9:8-9; Yesaya 43:3-5)

## Mutu 6

# Za Kugwa kwa Munthu, Tchimo ndi Chilango Chake

**1** Ngakhale Mulungu anamulenga munthu wopanda tchimo lililonse ndikumupatsa lamulo lomwe lidali lopereka moyo ngati alisunga ilo komanso [a]kubweretsa imfa pakuliphwanya ilo, koma munthu sadathe kulisunga lamuloli momwe amayenelera, [b]Satana mu uchinjelekezi wake podzera mwa njoka anamusocheleretsa Hava ndipo Hava anamukopa Adamu amene popanda kukakamizidwa anadya ndi kuchimwira lamulo la chilengedwe chawo ndi kuphwanya lamulo lomwe lidapatsidwa kwa iwo kuti asadye chipatso choletsedwa; ndipo ndi Mulungu yekha amene adali ndi mphamvu zololeza zochitikazi malingana ndi nzeru Zake ndi uphungu wake kwa ulemelero wake.

([a]Genesis 2:16-17; [b]Genesis 3:12-13; 2 Akorinto 11:3)

**2** Makolo athu oyamba, chifukwa cha tchimo ili adagwa ku [c]chiyero ndi chiyanjano chawo ndi Mulungu, [d]chimodzimodzinso ife mwa makolo athuwa tidagwa nawo ku chiyero ndi chiyanjano ndi Mulungu ndipo imfa inadza pa onse: [e]onse kukhala okufa m'machimo ndi kukhala oipitsidwa m'makhalidwe athu onse a kuthupi ndi mu mzimu.

([c]Aroma 3:23; [d]Aroma 5:12, [e]Tito 1:15; Genesis 6:5;
Yeremiya 17:9; Aroma 3:10-19)

**3** Mulungu posankha iwo kukhala [f]oyimilira mtundu wonse wa anthu, tchimo lawo, ndi kuonengeka kwa chilengedwe kwao kudapatsidwa kwa mibadwo yonse yomwe inabwera kutsatira iwo, ndipo ngakhale lero lino anthu [g]amabadwabe ochimwa, ndi mu chilengedwe chawo ana a [h]mkwiyo, akapolo a tchimo, [f]imfa ndi ziphinjo zosiyanasiyana, za kuuzimu, za padziko lapansi kapena za muyaya, malire ake Yesu Khristu [k]akamasule zimenezi.

([f]Aroma 5:12-19; 1 Akorinto 15:21-22,45,49; [g]Masalmo 51:5; Yobu 14:4;
[h]Aefeso 2:3; [f]Aroma 6:20, 5:12; [k]Ahebri 2:14-15; 1 Atesalonika 1:10)

**4** Kuchokera ku kuipitsidwa uku, anthu ife [l]timakhala otsutsana ndi chilichonse chabwino ndi cholondola, komano timakhala okonda zonse zoipa "ndipo zochimwa zathu zonse [m]zimachokera kudzera mwa kuonongekaku.

([l]Aroma 8:7; Akolose 1:21; [m]Yakobo 1:14-15; Mateyu 15:19)

**5** Kuonongeka kwa chikhalidwe m'moyo uno [n]kumatsalirabe mwa anthu opulumutsidwa, ngakhale zitakhala zokhululukidwa ndi kuthetsedwa ndi mphamvu ya Yesu zonsezi ndi [o]zochimwa ndithu.

([n]Aroma 7:18,23; Mlaliki 7:20; 1 Yohane 1:8;
[o]Aroma 7:23-25; Agalatiya 5:17)

## Mutu 7

# Za Chipangano cha Mulungu

**1** Pali kusiyana kwakukulu pakati pa Mulungu ndi munthu amene anamulenga, mwakuti ngakhale tikuyenera kumumvera Iye ngati mlengi wathu, sitingathe kupeza mphoto ya moyo kupatula mwa [a]kufuna kwa Iye Mulungu mwini kutifikira ife pansi pano, kumene Iye anakondwera kuti aonetsere popereka pangano. ([a]Luka 17:10; Yobu 35:7-8)

**2** Popeza munthu anadzibweretsera pa iye yekha [b]thembelero la chilamulo pamene anagwa, chinamkondweretsa Mulungu kupanga

chipangano cha chisomo, momwe Iye amapereka mwa ulere [c]moyo ndi chipulumutso mwa Yesu Khristu kwa ochimwa, powalamulira kuti akakhulupilire mwa Iye kuti akapulumutsidwe; ndi [d]kulonjeza kuti apereka kwa onse amene anaikidwiratu ku moyo wosatha, Mzimu Wake Woyera kuti ukathe kupatsa iwo kufuna ndi kuthekera kokhulupilira.

([b]Genesis 2:17; Agalatiya 3:10; Aroma 3:20-21; [c]Aroma 8:3; Mariko 16:15-16; Yohane 3:16; [d]Ezekieli 36:26-27; Yohane 6:44-45; Masalimo 110:3)

**3** Chipanganochi chinabvumbulutsidwa mu Uthenga wa Bwino; poyambilira kwa Adamu mu lonjezo la chipulumutso kudzera mu [e]mbewu ya mzimayi, kutsatira apo chinabvumbulutsidwa mu njira zina zambiri mpakana [f]kuzindikira kwake kokwanira mu Chipangano Chatsopano; ndipo kunakhazikitsidwa mu chipangano *chamuyaya chimenechi momwe mgwirizano udachitika pakati pa Tate ndi Mwana pa za kuwombola kwa anthu osankhidwa; ndipo ndi mwa chisomo chokha cha panganoli kuti m'badwo wonse wochokera mwa Adamu wochimwa [g]unapulumukira ndi kupeza moyo ndi mdalitso wa muyaya, pakuti munthu alibiletu kuthekera kolandilidwa pa maso pa Mulungu ngati momwe Adamu adaliri asanachimwe.

([e]Genesis 3:15; [f]Ahebri 1:1; *2 Timoteo 1:9; Tito 1:2; [g]Ahebri 11:6,13; Aroma 4:1-2, ndi ndime zotsatira; Machitidwe 4:12; Yohane 8:56)

## Mutu 8

# Za Khristu Mkhala Pakati

**1** Chinamkondweretsa Mulungu, mu cholinga chake, kuti asankhe ndi kuzoza Ambuye Yesu, Mwana wake Yekha, molingana ndi chipangano cha iwo awiri, kuti akhale mkhala [a]pakati wa Mulungu ndi munthu; [b]Mneneri, [c]wa Msembe ndi [d]Mfumu, Mutu ndi Mpulumutsi wa Mpingo ndi amene ali mwini wa zonse, wogamula dziko lonse, amene kuyambira kale lonse [e]adampatsa anthu onse kukhala mbewu yake, ndipo mwa Iye kukhala owomboledwa, oyitanidwa, olungamitsidwa, opatulidwa ndi otamandika.

([a]Yesaya 42:1; 1 Petro 1:19-20; [b]Machitidwe 3:22; [c]Ahebri 5:5-6; [d]Masalmo 2:6; Luka 1:33; Aefeso 1:22-23; Ahebri 1:2; Machitidwe 17:31; [e]Yesaya 53:10; Yohane 17:6; Aroma 8:30)

**2** Mwana wa Mulungu, wachiwiri wa mwa utatu woyera, yemwe ali Mulungu, kuwala kwa ulemelero wa Ambuye, amene ali chimodzimodzi ndi adalenga dzikoli, amene amasunga dzikoli pamodzi ndi kulamulira

zonse zomwe Iye adalenga, pamene nthawi idakwana adadzitengera pa Iye yekha [f]thupi ngati la munthu, koma [g]opanda uchimo wina uliwonse; nabadwa mwa Mzimu Woyera mwa viligo Maria, Mzimu Woyera anabwera pa iye ndipo mphamvu za Mulungu wa mphamvu zonse idamuvindikira iye, ndipo [k]mudapangidwira kuchokera mwa mzimayi mtundu wa Ayuda, mbewu ya Abrahamu ndi Davide malingana ndi Malemba, ndi kuti makhalidwe awiri adaikidwa pamodzi mwa munthu m'modzi popanda kusintha kulikonse kapena kusokoneza kulikonse; makhalidwe ake anali a munthu ndi Mulungu koma amodzi mwa Yesu [i]Khristu mkhala pakati yekhayo wa pakati pa Mulungu ndi munthu.

([f]Yohane 1:14; Agalatiya 4:4; [g]Aroma 8:3; Ahebri 2:14,16-17; 4:15; Mateyu 1:22-23; [k]Luka 1:27,31,35; [i]Aroma 9:5; 1 Timoteo 2:5)

**3** Ambuye Yesu Khristu mchikhalidwe chawo cha umunthu cholumikizidwa ndi cha umulungu, mwa Mwana, anali opatulika ndi ozozedwa [k]ndi Mzimu Woyera, wokhala nawo mwa Iye [l]kudzadza kwa nzeru ndi kudziwa; ndipo mwa iye Mulungu anakondwera kuti [m]kudzadza konse kukhale mwa Iye, mwa iye kukhala [n]opatulika, osaononga, osaipitsidwa, wodzadza [o]ndi chisomo ndi chilungamo kuti akathe kukhala wokwanira ndi wothekera kugwira ntchito ya [p]mkhalapakati ndi chilimbikitso; udindo uwu sadadzipatse yekha koma [q]adayitanidwa ndi Atate ake amene adapereka [r]mphamvu zonse ndi chigamulo chonse m'manja mwake ndi kumumpatsa lamulo kuti akachite chimodzimodzi.

([k]Masalmo 45:7; Machitidwe 10:38; Yohane 3:34; [l]Akolose 2:3; [m]Akolose 1:19; [n]Ahebri 7:26; [o]Yohane 1:14; Ahebri [p]7:22; [q]Ahebri 5:5; [r]Yohane 5:22,27; Mateyu 28:18; Machitidwe 2:36)

**4** Ntchito iyi Ambuye Yesu [s]anatenga mosakakamizidwa, ndipo anagwira ntchitoyi ali pansi pa lamulo [t]ndipo anakwaniritsa lamulo, ndikukalandira [u]chilango choyenera ife chomwe ife timayenera kulandira, koma Iye anakhala [x]tchimo m'malo mwa ife; kupilira zisoni zonse [y]mu uzimu wake, ndi kupilira zowawa zonse mthupi lake; anapachikidwa ndi kufa, ngakhale anali wakufa koma Iye sanaone [z]chibvundi, tsiku [a]lachitatu anauka kwa akufa ndi [b]thupi lomwelo lomwe adasautsika nalo, ndi lomwenso [c]adakwera nalo kumwamba kumeneko anakhala ku dzanja la manja la Mulungu Atate, [d]kupempherera anthu ake, ndipo [e]adzabweranso kuzaweruza anthu ndi angelo pakutha kwa dzikoli.

([s]Masalmo 40:7-8; Ahebri 10:5-10; Yohane 10:18; [t]Agalatiya 4:4; Mateyu 3:15; [u]Agalatiya 3:13; Yesaya 53:6; 1 Petro 3:18; [x]2 Akorinto 5:21; [y]Mateyu 26:37-38; Luka 22:44; Mateyu 27:46; [z]Machitidwe 13:37; [a]1 Akorinto 15:3-4; [b]Yohane 20:25,27;

([c]Mariko 16:19; Machitidwe 1:9-11; [d]Aroma 8:34; Ahebri 9:24; Machitidwe 10:42; Aroma 14:9-10; Machitidwe 1:11; 2 Petro 2:4)

**5** Ambuye Yesu mwa kumvera kwao ndi kukhala nsembe yomwe kudzera mwa Mzimu wa muyaya anapereka kamodzi konse ndi [f]kukwaniritsa chilungamo cha Mulungu, anapezera chiyanjanitso ndipo anagulira malo mu ufumu wa muyaya wa kumwamba [g]kwa anthu onse omwe anapatsidwa kwa Iye ndi Atate.

([f]Ahebri 9:14, 10:14; Aroma 3:25-26; [g]Yohane 17:2; Ahebri 9:15)

**6** Ngakhale mtengo woombolera anthu unalipilidwa ndi Khristu pakubwera kwake kudzakhala ngati munthu pansi pano, *tidziwe kuti ngakhale anthu a m'Chipangano Chakale adapindulanso nawo ku nsembeyi; izi zimaonetseredwa kalelo kudzera mu zithunzithunzi ndi zitsanzo za nsembe zomwe zinali kuonetsera za mbeu yomwe idzawononge mutu wa njoka; [h]ndi mwana wa nkhosa wophedwa kuyambira makhazikidwe a dziko lapansi, [i]amene ali yemweyo dzulo, ndi lero ndi ku nthawi zonse.

(*2 Akorinto 4:10; Ahebri 4:2; 1 Petro 1:10-11; [h]Chivumbulutso 13:8; [i]Ahebri 13:8)

**7** Khristu pa ntchito ya mkhalapakati amachita molingana ndi makhalidwe ake onse awiri, khalidwe lililonse palokha kuchita moyenerera; koma chifukwa cha umodzi wa umunthu zochita za khalidwe lina zimanenedwa [k]kukhala za khalidwe lina.

([k]Yohane 3:13; Machitidwe 20:28)

**8** Kwa onse amene Yesu adawapezera chiwombolo cha muyaya Iye mosakayikira [l]amawadziwitsa ichi, amawapempherera, kuwayanjanitsa kwa Iye yekha mwa Mzimu Woyera, [m]kuwaonetsera kudzera M'mau ake zozizwa za chipulumutso, kuwakopa kuti akakhulupilire ndi kumvera, [n]kutsogolera mitima yawo ndi Mawu ndi Mzimu ndi [o]kugonjetsa adani onse ndi mphamvu zake ndi nzeru zake, mu njira zomwe zili chimodzimodzi ndi [p]ndondomeko ya chipulumutso, zonse za ulere ndi chisomo chokhachokha, popanda ubwino uliwonse unaonedwa mwa anthu kuti akapeze chisomo.

([l]Yohane 6:37; 10:15-16; 17:9; Aroma 5:10; [m]Yohane 17:6; Aefeso 1:9; 1 Yohane 5:20; [n]Aroma 8:9,14; [o]Masalmo 110:1; 1 Akorinto 15:25-26; [p]Yohane 3:8; Aefeso 1:8)

**9** Ntchito ya mkhalapakati pa Mulungu ndi anthu ikuyenerera [q]Yesu yekha amene ali mneneri, wa nsembe, ndi Mfumu wa Mpingo wa

Mulungu; ndipo sipangakhale gawo kapena thunthu lonse la ntchitoyi lomwe lingapatsidwe kwa munthu wina. ([q]1 Tim 2:5)

**10** Kunena ndondomeko ya ntchito ndi maudindowa ndi kofunikira; chifukwa cha [r]kusadziwa kwathu, tikufunikira ntchito yake ngati mneneri; chifukwa cha kusiyanitsidwa kwathu ndi [s]kusalungama kwa ntchito zathu, tikufunikira Iye ngati Wansembe kuti atiyanjanitse ife ndi kutibweretsa ife ololedwa pa maso pa Mulungu; chifukwa cha kusathekera kwathu kutembenukira kwa Mulungu, kuti akatipulumutse ndi kutiteteza kwa adani athu a kuuzimu, tikufunikira Iye ngati mfumu akatilanditse ife, kutikokera ife, [t]kutitsimikizizira ife ndi kutisungira ife ku ufumu wa kumwamba.

([r]Yohane 1:18; [s]Akolose 1:21; Agalatiya 5:17;
[t]Yohane 16:8; Masalmo 110:3; Luka 1:74-75)

## Mutu 9

# Za Ufulu wa Chifuniro cha Munthu

**1** Mulungu analenga chifuniro cha munthu ndi kuthekera kochita zinthu mwa kufuna kwake popanda [a]kukakamizidwa kuchita chabwino kapena choipa. ([a]Mateyu 17:12; Yakobo 1:14; Deuteronomo 30:19)

**2** Munthu pamene anali mu kusalakwa kwake, anali ndi ufulu ndi kuthekera kofuna ndi kuchita zomwe zinali [b]zabwino ndi zomusangalatsa Mulungu, koma iye anali wotheka [c]kusinthika mokuti zinali zotheka kuti agwe. ([b]Mlaliki 7:29; [c]Genesis 3:6)

**3** Munthu, pamene anagwa mu uchimo adataya kuthekera [d]kulikonse kochita zabwino mu uzimu zoyendera limodzi ndi chipulumutso, choncho ngati munthu wakuthupi wokhala ndi udani ndi chilichonse chabwino, ndi [e]wokufa mu uchimo, alibe kuthekera [f]kodzisintha yekha, kapena kudzikonzekeretsa kuti apulumuke.

([d]Aroma 5:6, 8:7; [e]Aefeso 2:1,5 [f]Tito 3:3-5; Yohane 6:44)

**4** Pamene Mulungu wasintha munthu, ndi kumubweretsa ku moyo wa chisomo, [g]amamumasula ku ukapolo wa tchimo, ndipo mwa chisomo chake chokha amamupangitsa kuti akhale nawo [h]ufulu wochita mwa uzimu zinthu zabwino; komabe chifukwa cha zoipa zomwe [i]zatsalira mwa iye, samapanga zonsezi molongosoka, kapena kufuna kuchita zabwino zokha, komanso amakhala akufuna kuchita zoipa.

([g]Akolose 1:13; Yohane 8:36; [h]Afilipi 2:13; [i]Aroma 7:15,18-19,21,23)

**5** Chifuniro cha munthu ichi chimakhala ndi ufulu [k]wokwanira komanso wosasinthika kuti chikwanitse kuchita zabwino zokhazokha mu moyo wa ulemelero wokha. (Aefeso 4:13)

## Mutu 10

# Za Kukwaniritsidwa kwa Kuitana

**1** Kwa onse amene Mulungu anawaitanira ndi kuwakonzera ku moyo, ali wosangalatsidwa, mu nthawi yomwe anaisankha [a]kuitana onse kudzera M'mawu ake ndi Mzimu wake ku chikhalidwe cha uchimo ndi imfa chomwe ali mwa chilengedwe chawo, kuwaitanira ku chisomo ndi chipulumutso [b]mwa Yesu Khristu, kuunikira malingaliro awo mu uzimu ndi mwachipulumutso [c]kumvetsetsa zinthu za Mulungu, kuwachotsera [d]mtima wa mwala, ndi kuwapatsa mtima wa mnofu; kukonzanso zifuniro zawo, ndi mphamvu zake kuwalondolera [e]ku zomwe zili zabwino, ndi kuwakokera kwa Yesu Khristu, ngakhale iwo akubwera mosakakamizidwa, ndi [f]chisomo chokha chomwe chikuwachititsa iwo kuti atero.

([a]Aroma 8:30; 11:7; Aefeso 1:10-11; 2 Atesalonika 2:13-14; [b]Aefeso 2:1-6; [c]Machitidwe 26:18; Aefeso 1:17-18; [d]Ezekiyele 36:26; [e]Deuteronomo 30:6; Ezekiyele 36:27; Aefeso 1:19; [f]Masalmo 110:3; Nyimbo 1:4)

**2** Kuitana uku ndi kwa chisomo cha ulere cha Mulungu yekha basi, [g]popanda chilichonse choonedwa mwa munthu, kapena mphamvu za munthu kuthandizira chisomo chake, [h]koma munthu kukhala osapanga kanthu ndi kukhala wokufa mu uchimo ndi zolakwika, mpakana ataukitsidwa ndi kupangidwa mwatsopano ndi Mzimu woyera, potero azatha kuyankha kuitana kumeneku ndi kulandira chisomo chomwe chimaperekedwa mu kuitanaku, kudzera mu [i]mphamvu yomwe inaukitsa Yesu kwa akufa.

([g]2 Timoteo 1:9; Aefeso 2:8; [h]1 Akorinto 2:14; Aefeso 2:5; Yohane 5:25; [i]Aefeso 1:19-20)

**3** Osankhidwa achichepere amene amafa ali ana, [k]amakonzedwanso ndi kupulumutsidwa ndi Khristu Yesu kudzera mwa Mzimu Woyera; amene amagwira pamene ndi kumene ndi [l]momwe amafunira; momwemo ndi onse amene ali osankhidwa, amene sangathe kuitanidwa mwachikunja ndi mawu a Mulungu. ([k]Yohane 3:3,5-6; [l]Yohane 3:8)

**4** Ena sanasankhidwe, ngakhale mawu a Mulungu ali kuwaitana, [m]akhozanso kugwiritsidwa ntchito ndi Mzimu Woyera, koma kupezeka

kuti Mulungu sanawasankhe iwo ndi kuwakokera kwa Iye, anthu amenewa sangathe [n]kubwera kwa Yesu, kotero sangathe [o]kupulumutsidwa; chimodzimodzinso amene samalandira chipembezo cha chi Khristu sangapulumutsidwe; ngakhale iwo atachita mosamala zomwe zipembezo zawo zimawauzira.

([m]Mateyu 22:14, 13:20-21; Ahebri 6:4-5; [n]Yohane 6:44-45,65; 1 Yohane 2:24-25; [o]Machitidwe 4:12; Yohane 4:22; 17:3)

# Mutu 11
# Za Kuyesedwa Olungama

**1** Amene Mulungu anawaitana, Iye mwa ulere [a]anawayesanso olungama, osati pakuika chiyero mwa anthuwa koma [b]pakuwakhululukira machimo awo ndi kuwawerengera komanso kuwabvomera ngati [c]olungama; osati chifukwa cha zintchito zawo koma chifukwa cha Yesu Khristu yekha; osawerengera chikhulupiliro pachokha, kukhulupilira kwao, kapena [d]kumvera kwao kulikonse ngati chiyero chawo; koma kuwerengera pa iwo kumvera kwa chilamulo chonse kwa Yesu Khristu, ndi kumvera kwa Iye kufikira ku imfa yake kuti iwo akakhale ndi chiyero, ndipo iwo [e]polandira ndi popumula mwa Iye ndi chiyero chake, kudzera mwa chikhulupiro osati cha mwa iwo okha, koma mphatso yochokera kwa Mulungu.

([a]Aroma 3:24, 8:30; [b]Aroma 4:5-8; Aefeso 1:7; [c]1 Akorinto 1:30-31; Aroma 5:17-19; [d]Afilipi 3:8-9; Aefeso 2:8-10; [e]Yohane 1:12; Aroma 5:17)

**2** Kotero chikhulupiliro, kulandira ndi kutsamira pa Yesu ndi chiyero chake, ndi njira [f]yokhayo yomwe munthu angalungamitsidwire, koma chikhulupiliro sichikhala pachokha mwa munthu wolungamitsidwa, chimayenda limodzi ndi zisomo za chipulumutso zina zonse, ndipo si chakufa, koma chimagwira ntchito mwa [g]chikondi.

([f]Aroma 3:28; [g]Agalatiya 5:6; Yakobo 2:17, 22, 26)

**3** Khristu, pakumvera kwake ndi imfa yake, analipira ngongole yonse ya amene ali olungamitsidwa; ndipo kudzera mwa nsembe ya Iye yekha mu mwazi wa pa mtanda wake, analandira chilango chomwe chimayenera anthuwo ndi kukwaniritsa [h]chilungamo cha Mulungu m'malo mwao; komabe ngakhale anaperekedwa ndi Atate kwa iwo, komanso kumvera kwake ndi kukwaniritsa kwake kwa zofuna za Mulungu zomwe zinalandiridwa ndi Mulungu m'malo mwao, [i]mwaulere, osati chifukwa cha kalikonse mwa iwo, kulungamitsidwa kwao ndi kwa chisomo chaulere

ndi cholinga choti chilungamo cha Mulungu ndi chisomo chake chodzadza [k]zikatamandike pa kulungamitsidwa kwa ochimwa.

([h]Ahebri 10:14; 1 Petro 1:18-19; Yesaya 53:5-6; [i]Aroma 8:32; 2 Akorinto 5:21; [k]Aroma 3:26; Aefeso 1:6-7, 2:7)

**4** Mulungu analamulira ku nthawi zosatha kuti [l]adzalungamitsa anthu osankhidwa, ndipo Khristu pa nthawi yoyenerera anafera machimo awo ndi [m]kuukanso kuti alungamitsidwe, komabe samalungamitsika paokha malire ake Mzimu Woyera, pa nthawi yoyenera, [n]ataika Khristu mwa iwo.

([l]Agalatiya 3:8; 1 Petro 1:2; 1Timoteo 2:6; [m]Aroma 4:25; [n]Akolose 1:21-22; Tito 3:4-7)

**5** Mulungu amapitilira [o]kukhululukirabe machimo a anthu omwe alungamitsidwa, ngakhale sizingatheke kuti iwo agwe kuchoka ku [p]kulungamitsidwa, komabe iwo chifukwa cha kuchimwa kwao akhoza [q]kulangidwa ndi Mulungu monga Tate wawo, ndipo ku nyengo zoterezi kuwala kwa Mulungu Tate wawo sikumaonekera iwo, malire ake [r]atadzichepetsa, kubvomereza machimo awo, kupempha chikhululukiro, ndi kubwezeretsedwa ku chikhulupiro ndi kulapa kwao.

([o]Mateyu 6:12;1 Yohane 1:7,9; [p]Yohane 10:28 [q]Masalimo 89:31-33; [r]Masalimo 32:5; Masalimo 51; Mateyu 26:75)

**6** Kulungamitsidwa kwa anthu okhulupilira pansi pa Chipangano Chakale kunali [s]kofanana ndi kulungamitsidwa kwa anthu okhulupilira a Chipangano Chatsopano. ([s]Agalatiya 3:9; Aroma 4:22-24)

## Mutu 12

# Za Kukhala Mwana wa Mulungu

**1** Onse amene ali olungamitsidwa, Mulungu anawapatsa mwayi, mwa Yesu ndi chifukwa cha mwana wake Khristu Yesu, kuti iwo akapeze nawo chisomo [a]chokhala ana a Mulungu, pamene iwo amatengedwa nakhala m'modzi mwa anthu okhala ndi ufulu ndi [b]zokoma zina za ana a Mulungu, ndipo amakhala ndi [c]dzina lake pa iwo, [d]amalandira mzimu wakukhala mwana wa Mulungu, [e]amakhala ndi kuthekera kofikira ku mpando wa chisomo mopanda mantha ndipo iwo afuula "Abba, Atate," amachitidwa [f]chisoni, [g]amatetezedwa, [h]amasamalilidwa ndi [i]kulangidwa ndi iye pamene alakwitsa, [k]samatayidwa ayi, [l]koma kusungidwabe mpakana tsiku lakuwomboledwa ndi kuzapeza malonjezano [m]a kukhala ndi moyo wosatha.

([a]Aefeso 1:5; Agalatiya 4:4-5; [b]Yohane 1:12; Aroma 8:17; [c]2 Akorinto 6:18; Chivumbulutso 3:12; [d]Aroma 8:15; Agalatiya 4:6; Aefeso 2:18; [f]Masalmo 103:13; [g]Miyambo 14:26; [h]1 Petro 5:7; [i]Ahebri 12:6; [k]Yesaya 54:8-9; Maliro 3:31; [l]Aefeso 4:30; [m]Ahebri 1:14; 6:12)

# Mutu 13
# Za Kuyeretsedwa

**1** Amene ali olunzanitsidwa mwa Yesu, oitanidwa ndi obadwanso mwa tsopano, okhala ndi mtima wa tsopano ndi mzimu wa tsopano wolengedwa mwa iwo chifukwa cha imfa ya Yesu ndi kuuka kwake, iwo alinso [a]opatulika mwa mphamvu yomweyi kudzera mwa [b]Mawu ake ndi Mzimu wokhala mwa iwo; [c]ulamuliro wonse wa tchimo unaonongedwa, ndipo [d]zilakolako zambiri zimakhala zikuchepera chepera mphamvu mpaka zidzafa mwa iwo, ndipo anthuwa [e]amalimbikitsidwa mu zisomo zopulumutsa, kuti akakhale ndi machitidwe [f]opatulika, omwe popanda kutero palibe adzaone Mulungu.

([a]Machitidwe 20:32; Aroma 6:5-6; [b]Yohane 17:17; Aefeso 3:16-19; 1 Atesalonika 5:21-23; [c]Aroma 6:14; [d]Agalatiya 5:24; Akolose 1:11; [f]2 Akorinto 7:1; Ahebri 12:14)

**2** Kuyeretsedwa uku kumachitika mwa munthu wa [g]thunthu ngakhale mosakwanira [h]m'moyo uno; chibvundi chimapezekabe m'mbali ina iliyonse, zomwe zimachititsa kuti pakhale [i]nkhondo; thupi kulimbana ndi Mzimu ndipo Mzimu kulimbana ndi thupi.

([g]1 Atesalonika 5:23; [h]Aroma 7:18,23; [i]Agalatiya 5:17; 1 Petro 2:11)

**3** Mu nkhondo imeneyi, ngakhale kwa kanthawi zoola za kuthupi zikhoza [k]kupambana, munthu [l]wobadwanso wa kuuzimu adzagonjetsabe basi kudzera mwa Mzimu woyeretsa mwa Yesu; choncho oyera mtima amakula m'chisomo, akukwaniritsa chiyero powopa Mulungu, [m]akuyesetsa kufikira moyo wa kumwamba pa kumvera malamulo onse omwe Khristu yemwe ali Mutu ndi Mfumu, walamula m'mawu ake.

([k]Aroma 7:23; [l]Aroma 6:14; [m]Aefeso 4:15-16; 2 Akorinto 3:18, 7:1)

# Mutu 14
# Za Chikhulupiliro Chopulumutsa

**1** Chisomo cha chikhulupiliro, ndi chomwe anthu osankhidwa amakhala ndi kuthekera kokhulupilira kopulumutsa miyoyo yawo, ndi ntchito ya Mzimu wa Khristu [a]m'mitima yawo, ndipo imagwirika pa munthu kudzera mu utumiki wa [b]Mawu a Mulungu, ndiponso pa utumiki wa ubatizo ndi m'gonero wa Ambuye, pemphero ndi njira zina zomwe anakonza Mulungu, chisomochi chimakula ndi [c]kulimbikitsidwa.

(2 Akorinto 4:13; Aefeso 2:8; [b]Aroma 10:14,17; [c]Luka 17:5; 1 Petro 2:2; Machitidwe 20:32)

**2** Chifukwa cha chikhulupiliro ichi, Mkristu amakhulupilira kuti [*]chilichonse chomwe chinalembedwa M'mawu a Mulungu ndi choona ndikuti Mulungu akalamulire kudzera Mawuwa. Ndiponso mwa iwo muli [d]kupambana kuposa zolembedwa zonse pa dziko lino, pakuti Mawuwa amaonetsera ulemelero wa Mulungu mu Makhalidwe ake, kupambana kwa Khristu mu chikhalidwe chake ndi mu udindo wake ndi mphamvu ya Mzimu Woyera mu ntchito yake; ndipo Mkhristu amakhala ndi kuthekera [e]kodzikhuthula moyo wake pa chilungamo chomwe wakhulupilirapo; ndiponso molingana ndi momwe Mawu a Mulungu [f]akulamulira pa ndime ina iliyonse; kumvera pamene [g]akuchenjezedwa, kukumbatira [h]malonjezo a Mulungu pa moyo uno ndi womwe uli mkudza; koma mfundo za machitidwe a chikhulupiliro chopulumutsa ali olumikizana mwa thunthu ndi Yesu Khristu, kubvomera, kulandira ndi kupumula pa [i]Iye yekha pa kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ndi moyo wosatha, kudzera mu chipangano cha chisomo.

(*Machitidwe 24:14; [d]Masalmo 19:7-10; 119:72; [e]2 Timoteo 1:12; [f]Yohane 15:14; [g]Yesaya 66:2; [h]Ahebri 11:13; [i]Yohane 1:12; Machitidwe 16:31; Agalatiya 2:20; Machitidwe 15:11)

**3** Chikhulululupiro ichi, ngakhale chimakhala m'miyezo yosiyanasiyana, ndipo chikhoza kukhala chofooka[k] kapena cha ngwiro, koma chofunikira ndi mtundu wake wa chikhulupirochi osati kachulukidwe ka chikhulupiro. Choncho ngakhale nthawi zina chikhulupirochi chimafooketsedwa ndi kukumana ndi zovuta, chimapezabe [m]chipambano, kukula muzokwaniritsa za [n]chitsimikizo kudzera mwa Yesu amene ali woyambitsa [o]ndi mathero a chikhulupiro chathu.

([k]Ahebri 5:13-14; Mateyu 6:30; Aroma 4:19-20; [l]2 Petro 1:1; Aefeso 6:16; 1 Yohane 5:4-5; Ahebri 6:11-12; Akolose 2:2; [o]Ahebri 12:2)

# Mutu 15
# Za Kulapa Kotengera Munthu ku Moyo ndi Chipulumutso

**1** Osankhidwa amene amatembenuka mtima atakula kale, atakhalapo mu [a]chilengedwe cha thupi, momwe anali kutumikira zilakolako ndi zokondweretsa zamitundumitundu, Mulungu pakuwaitana kwao amawapatsa kulapa kowatengera ku moyo. ([a]Tito 3:2-5)

**2** Pakuti palibe munthu amene amachita zabwino ndi [b]kusachimwa, anthu amakhalidwe abwino, akhoza kugwa m'machimo chifukwa cha mayesero; Mulungu mchipangano cha chisomo, mwa chifundo anapereka njira yokuti okhulupilira amene achimwa ndi kugwa akathe [c]kutembenuka kudzera mu kulapa kotengera munthu ku chipulumutso.

([b]Mlaliki 7:20; [c]Luka 22:31-32)

**3** Kulapa kopulumutsa kumeneku ndi chisomo [d]chosintha munthu, pamene munthu, motsogozedwa ndi Mzimu Woyera wazindikiritsidwa za kuipa kosiyana siyana kwa machimo ake, mwa chikhulupiro mwa Yesu, amadzichepetsa kamba ka machimowo ndi chisoni cha umulungu, ndi kudana nalo tchimo ndi kunyasidwa ndi iye mwini, [e]wapempha chikhululukiro ndi mphamvu ya chisomo, ndi cholinga ndi kuyetsetsa, mwa Mphamvu zopatsidwa ndi Mzimu Woyera, [f]kuyenda pa maso pa Mulungu mu zinthu zonse zokondweretsa.

([d]Zekariya 12:10; Machitidwe 11:18; [e]Ezekieli 36:31;
2 Akorinto 7:11; [f]Masalimo 119:6,128)

**4** Pakuti tikuyenera kulapa masiku onse a moyo wathu, chifukwa cha thupi lathu, ndi zilakolako zake, ndi udindo wa munthu aliyense kulapa tchimo [g]lililonse lodziwika mwa iye palokha palokha.

([g]Luka 19:8; 1Timoteo 1:13,15)

**5** Iyo ndiyo njira yomwe Mulungu anaperekera kudzera mwa Khristu mu chipangano cha chisomo kuti okhulupilira akasungike kufikira ku chipulumutso; kuti ngakhale palibe tchimo lomwe liri laling'ono koma machimo onse ayenera chilango, palibenso tchimo lokulitsitsa kuti likabweretse [h]chionongeko pa aliyense amene [i]walapa; izi ndizo zotichititsa kulalikira za kulapa tsiku ndi tsiku.

([h]Aroma 6:23; [i]Yesaya 1:16-18, 55:7)

# Mutu 16
# Za Zintchito za Bwino

**1** Zintchito zabwino ndi zokhazo zomwe Mulungu [a]analamulira M'mawu Opatulika, osati zimene sizili zololedwa ndi mawu a Mulungu kapena zopangidwa ndi anthu chifukwa cha kusadziwa, [b]kapena pofuna kuonetsera malingaliro abwino.

([a]Mika 6:8; Ahebri 13:21; [b]Mateyu 15:9; Yesaya 29:13)

**2** Ntchito zabwino izi, zikachitidwa momvera malamulo a Mulungu, umakhala umboni ndi zipatso za chikhulupiliro chokhadzikika ndi [c]choona; ndipo mwa ntchito zimenezi okhulupilira amaonetsa [d]kuthokoza kwao, kulimbikitsa [e]chitsimikizo chawo, kulimbitsa [f]anthu ena okhulupilira, kuvala chizindikiro chawo cha Uthenga Wabwino, kuletsa pakamwa a adani awo ndi kupereka ulemelero kwa [g]Mulungu, amene anawalenga mwa Yesu [h]kuti akagwire ntchito, ndikubala zipatso pa kuyenda mopatulika kuti pa mapeto pake akakhale ndi [i]moyo wosatha.

([c]Yakobo 2:18,22; [d]Masalmo 116:12-13; [e]1 Yohane 2:3,5; 2 Petro 1:5-11; [f]Mateyu 5:16; [g]1 Timoteo 6:1; 1 Petro 2:15; Afilipi 1:11; [h]Aefeso 2:10; [i]Aroma 6:22)

**3** Kuthekera kwao kochita ntchito zabwino sikuli mwa iwo okha koma chifukwa cha Mzimu [k]wa Khristu, kuti iwo akathe kukhala ndi kuthekera kochita choncho, pa mbali pa zisomo zomwe ali nazo kale, pali [l]kufunikira kwa Mzimu Woyera yemweyo, kuti akagwire ntchito mwa iwo, kufuna ndi kuchita molingana ndi zomsangalatsa Mulungu; koma iwo sakuyenera kulekelera ngati kuti sakuyenera kuchita ntchito iliyonse pokhapokha ngati pali ntchito yapadera ya Mzimu Woyera, koma akuyenera kukhala [m]olimbikira kubukitsa chisomo cha Mulungu chomwe chili mwa iwo.

([k]Yohane 15:4-5; [l]2 Akorinto 3:5; Afilipi 2:13; [m]Afilipi 2:12; Ahebri 6:11-12; Yesaya 64:7)

**4** Iwo amene mukumvera kwao amachita koposa, zomwe zili zotheka m'moyo uno, sangathe kuchita mopitilira mwezo wa momwe Mulungu amafuna kuti achite, [n]pakuti amapelewera pa zomwe amayenera kuti achite. ([n]Yobu 9:2-3; Agalatiya 5:17; Luka 17:10)

**5** Sitingathe kugula chikhulukiro kwa Mulungu kudzera mu zintchito zathu, chifukwa cha kusiyana kwa zintchitozi ndi ulemelero womwe uli mkudza, kusiyana kopanda malire kwa pakati pa Mulungu ndi anthufe, Mulungu amene mwa zintchito zathu sitingathe kukwaniritsa ngongole

ya [o]machimo athu, koma pamene tachita zomwe tingathe timakhala kuti tangochita ntchito yathu yomwe timayenera kugwira ndipo ndife akapolo osapindulitsa, ndipo chifukwa chokuti zintchitozi ndi zabwino, zimachokera kwa [p]Mzimu ndipo zimachitidwa ndi ife zimaipitsidwa [q]ndi kusakanizidwa ndi zofooka, ndi zosalungama, mokuti sizingathe kupilira kukhwima kwa chilango cha Mulungu.

([o]Aroma 3:20; Aefeso 2:8-9; Aroma 4:6; [p]Agalatiya 5:22-23; [q]Yesaya 64:6; Masalmo 143:2)

**6** Koma mopanda kukaikira umunthu wa anthu okhulupilira kukhala [r]ololedwa mwa Yesu, ntchito zawo zabwinonso zimabvomerezedwa mwa Iye, osati chifukwa chokuti padziko pano ali opanda cholakwika chilichonse pa maso pa Mulungu koma Mulungu amawayang'ana iwo kudzera mwa Mwana Wake Yesu, ndipo ali wosangalatsidwa kubvomera ndi kupereka mphotho kwa yense ali kuchita ntchito ndi [s]mtima wonse ngakhale amakhala ndi zofooka ndi zolakwika.

([r]Aefeso 1:6; 1 Petro 2:5; [s]Mateyu 25:21,23; Ahebri 6:10).

**7** Zintchito zopangidwa ndi anthu osatembenuka ngakhale kwa iwo zikhoza kukhala zomwe Mulungu akulamula ndipo zikhoza kukhala za phindu kwa iwo ndi anthu [t]ena; koma chifukwa chakuti zikuchitidwa ndi mtima womwe siunatsukidwe ndi [u]chikhulupiliro, kapena kuchita mosayenera momwe [x]Mau a Mulungu amafunira, kapena ndi cholinga chosayenera ndi ku [y]ulemelero wa Mulungu; izi zimakhala tchimo ndipo sizimasangalatsa Mulungu, ndipo sizimapangitsa munthu wothekera kulandira chisomo kuchokera kwa [z]Mulungu, ngakhale zili chonchi iwo kukhala opanda kuchita izi zimatengedwa ngati tchimo ndipo [a]sizisangalatsa Mulungu.

([t]2 Mafumu 10:30; 1 Mafumu 21:27,29; [u]Genesis 4:5; Ahebri 11:4,6; [x]1 Akorinto 13:1; [y]Mateyu 6:2,5; [z]Amosi 5:21-22; Aroma 9:16; Tito 3:5; [a]Yobu 21:14-15; Mateyu 25:41-43)

## Mutu 17

# Za Kupilira kwa Anthu Oyera Mtima

**1** Iwo amene Mulungu anawabvomera mwa Yesu Khristu, naitanidwa, nayeretsedwa ndi Mzimu Woyera, ndikupatsidwa chikhulupiliro cha mtengo wapatali cha osankhidwa ake, sangathe kwa thunthu kugweratu kuchoka ku chisomo, koma motsimikizika [a]adzapilirabe mpakana kumathero, ndikupulumutsidwa kwa muyaya, pakuti mphatso ndi kuitana

kwa Mulungu sizilapika, Iye amaperekabe kwa iwo, chikhulupiliro, kutembenuka mtima, chikondi, chimwemwe, chiyembekezo ndi zisomo zonse za Mzimu ku moyo wosatha; ngakhale namondwe ndi madzi osefukira zingabwere ndi kusautsa iwo, komabe izi sizidzawachotsa iwo pa maziko a pa thanthwe limene mwa chikhulupiliro iwo aimapo; ngakhale zili chonchi, kudzera mu kusakhulupilira ndi mayesero a Satana, kuwala kwa chikondi cha Mulungu kutha kwa kanthawi kukhala [b]kophimbika kwa iwo, koma Iye adakali chimodzimodzi, ndipo iwo adzakhala [c]otsimikizizika kuti asungidwabe ndi mphamvu ya Mulungu kufikira ku chipulumutso, komwe adzakondwelere ndi mphatso yawo yoguliridwa, atalembedwa pa dzanja lake, komanso maina awo atalembedwa m'buku la moyo kuyambira muyaya.

([a]Yohane 10:28-29; Afilipi 1:6; 2 Timoteo 2:19; 1 Yohane 2:19; [b]Masalimo 89:31-32; 1 Akorinto 11:32; [c]Malaki 3:6)

**2** Kupilira kwa anthu okhulupira uku sikumatengera ufulu wa chifuniro chawo, koma kumachokera pa kusasintha kwa momwe Mulungu analumulira [d]kusankhidwa kwao, kumachokera ku chikondi chaulere ndi chosasintha cha Mulungu Atate, kudzera mwa kuthekera ndi kupembedzera kwa Yesu Khristu, ndi [e]umodzi wa iwo ndi Iye, [f]lumbiro la Mulungu, kukhala kwa Mzimu Woyera mwa iwo, ndi [g]mbeu ya Mulungu mwa iwo ndi machitidwe a [h]chipangano cha chisomo; mwa zonsezi timaona kutsimikizizika ndi kusalakwika kwa zimenezi.

([d]Aroma 8:30; 9:11,16; [e]Aroma 5:9-10; Yohane 14:19; [f]Ahebri 6:17-18; [g]1 Yohane 3:9; [h]Yeremiya 32:40)

**3** Ngakhale iwo, kudzera m'mayesero a Satana ndi a dziko lapansi, kupitilira kwa zoipa zotsalira zili mwa iwo, ndi kulekelera kwa njira zozitetezera, atha kugwa [i]m'machimo osiyanasiyana, ndipo kwa kanthawi kupitilira kukhalabe m'machimowa, ndipo amapalamula [k]mkwiyo wa Mulungu ndi kukhumudwitsa Mzimu Woyera, amakhoza kuipitsa zisomo ndi zitonthozo zawo, kuumitsidwa mitima yawo, ndi chikumbumtima chawo kuonongeka, kulakwira ndi [m]kusautsa anzawo ena, ndi kuzibweretsera chigamulo pa iwo okha, koma ngakhale zonse zili chonchi iwo adzatha kulapanso ndi [o]kutembenuka ku zoipa ndi kukatetezedwa ku zoipa mpakana kumathero kudzera mwa Yesu Khristu.

([i]Mateyu 26:70,72,74; [k]Yesaya 64:5,9; Aefeso 4:30; [l]Masalimo 51:10,12; [m]Masalimo 32:3-4; [n]2 Samueli 12:14; [o]Luka 22:32,61-62)

# Mutu 18
# Za Chitsimikizo cha Chisomo ndi Chipulumutso

**1** Ngakhale anthu ooneka ngati okhulupilira ndi ena omwe siali otembenuka, akhonza kuzinamiza okha ali ndi chiyembekezo ndi kukonderedwa ndi Mulungu ndipo ali opulumutsidwa, [a]chiyembekezo chawo chidzatayika; pomwe onse amene akhulupiliradi mwa Yesu, ndikumukonda Iye ndi mtima wonse, ndikuyesetsa kuyenda ndi chikumbumtima chabwino pamaso pa Mulungu, m'moyo uno akhoza kukhala otsimikiza [b]kuti ali mu chisomo, ndipo akhoza kukondwerera mchiyembekezo cha ulemelero wa Mulungu chomwe sichizawachititsa iwo [c]manyazi.

([a]Yobu 8:13-14; Mateyu 7:22-23; [b]1 Jo 2:3; 3:14,18-19,21,24; 5:13; [c]Aroma 5:2,5)

**2** Kutsimikizika kumeneku si chikoka chokhadzikika pa [d]chiyembekezo chamalire, koma chomwe chili chosalakwika chokhadzikika pa mwazi ndi chiyero cha Yesu Khristu [e]choonetseredwa mu Uthenga Wabwino; komanso pa [f]umboni wa zisomo za Mzimu zomwe malonjezano anachitidwa m'mtima mwao, ndi kuchitira umboni kwa Mzimu wopangitsa ife kukhala ana [g]ake, kuchitira umboni ndi mzimu wathu kuti ndife ana a Mulungu; ndipo ngati chipatso chake kusunga mtima [h]wodzichepetsa ndi wopatulika.

([d]Ahebri 6:11,19; [e]Ahebri 6:17-18; [f]2 Petro 1:4-5,10-11; [g]Aroma 8:15-16; [h]1 Yohane 3:1-3)

**3** Chitsimikizo chosalakwika ichi sichimakhala chifukwa cha chikhulupiliro chathu, koma kuti munthu wokhulupiliradi akadikirebe ndi kukumana ndi zopinga zambiri iwo [i]asanafikirepo; koma kupatsidwa ndi Mzimu Woyera kuthekera kodziwa zinthu zapatsidwa kwa iwo mwa ulere ndi Mulungu, akhoza opanda mazindikiritso odabwitsa [k]kufikira ku zinthu izi; choncho ndi ntchito ya munthu aliyense wokhulupilira kukhala wolimbikira poonetsetsa kuti kuitana ndi kusankhidwa kwao kuli kotsimikizika, kuti chifukwa cha ichi mtima wake ukakule mu mtendere ndi chimwemwe mwa Mzimu Woyera, mu chikondi ndi kuthokoza kwa Mulungu, ndi mu mphamvu ndi chikondwerero mu ntchito za kumvera, [l]zipatso zoyenera za chitsimikizochi; [m]chomwe sichili chosendezera anthu ku zoipa.

([i]Yesaya 50:10; Masalmo 88; 77:1-12; [k]1 Yohane 4:13; Ahebri 6:11-12; [l]Aroma 5:1-2,5; 14:17; Masalmo 119:32; [m]Aroma 6:1-2; Tito 2:11-12,14)

**4** Anthu okhulupilira akhoza chitsimikizo cha kupulumuka kwawo kugwedezeka ndi kuchepetsedwa mu njira zosiyanasiyana, chifukwa cha[n] kulekelera mu kupilira kwao, pa [o]kugwa mu uchimo zomwe zimaononga chikumbumtima ndi kukhumudwitsa Mzimu Woyera, chifukwa cha mayesero [p]akulu, komanso Mulungu kuchotsera iwo [q]kuwala kwa nkhope yake, ndi kulolera ngakhale iwo amene amaopa Iye kuti akayende mu m'dima opanda kuwala, koma iwo amakhalabe ndi [r]mbeu ya Mulungu, ndi moyo [s]wa chikhulupiliro, chikondi kwa Yesu ndi a Khristu ena, kukhulupirika kwa mtima ndi chikumbumtima cha ntchito chomwe chifukwa cha ntchito ya Mzimu Woyera, chitsimikizo ichi ku nthawi yoyenera [t]chizatsitsimutsidwa, chomwenso chikhalire icho [u]chimawateteza iwo ku chikayiko.

([n]Nyimbo 5:2-3,6; [o]Masalmo 51:8,12,14; [p]Masalmo 116:11; 77:7-8; 31:22; [q]Masalmo 30:7; [r]1 Yohane 3:9; [s]Luka 22:32; [t]Masalmo 42:5,11; [u]Maliro 3:26-31)

## Mutu 19

# Za Chilamulo cha Mulungu

**1** Mulungu anapereka kwa Adamu lamulo lakumvera, lomwenso aliyense akuyenera kutsatira, lolembedwa [a]pamtima pake, ndiponso mwapaderadera lakuti asadye chipatso cha mtengo wodziwitsa chabwino ndi choyipa; chilamulo chomwe chinaika Adamu ndi mibadwo yonse yobwera pa mbuyo pake ku kumvera nthawi [b]zonse; nalonjeza moyo pakumvera lamuloli ndi kupereka chiopsezo cha imfa pamene lamuloli laphwanyidwa, ndipo Mulungu anampatsa mphamvu ndi kuthekera kosunga lamuloli.

([a]Genesis 1:27; Mlaliki 7:29; [b]Aroma 10:5; [c]Agalatiya 3:10,12)

**2** Lamulo lomwe poyamba linalembedwa pa mtima wa [d]munthu linapitilira kukhala lotsogolera m'chiyero pamene munthu anagwa, ndipo Mulungu analipereka pa phiri la Sinai mu malamulo [e]khumi, olembedwa pa miyala iwiri, malamulo anayi oyamba okhudzana ndi udindo wathu kwa Mulungu ndi ena asanu ndi limodzi okhudzana ndi udindo wathu kwa anthu ena. ([r]Aroma 2:14-15; [e]Deuteronomo 10:14)

**3** Pa mbali pa lamuloli, lotchedwa lamulo la chikhalidwe, Mulungu chinamkondweretsa kupereka kwa anthu aku Israeli lamulo la miyambo,

lomwe linali ndi malamulo osiyanasiyana omwe anali fanizo, ena a chipembezo, okhala ndi [f]chithunzithunzi cha Yesu Khristu, zisomo zake, machitidwe ake, mazunzo ake ndi zopindula zake; mwapaderanso lamuloli linali likuphunzitsa udindo wa [g]makhalidwe, malamulo a miyambo onsewa omwe anali osankhidwa mpaka nthawi yakukonzanso, [h]anachotsedwa ndi kutengedwa ndi Yesu Khristu Mesiya woona, yekhayo amene amapereka chilamulo, amene anapatsidwa mphamvu yochita zimenezo kuchokera kwa Atate.

([f]Aheberi 10:1; Akolose 2:17; [g]1 Akorinto 5:7;
[h]Akolose 2:14,16-17; Aefeso 2:14,16)

**4** Kwa iwonso kunapatsidwa malamulo osiyanasiyana a za chilungamo, amene anathetsedwa pamodzi ndi makhalidwe a anthu anthawi imeneyo, iwo siali okakamiza aliyense masiku ano, koma ndi [i]ongotiunikira.

([i]1 Akorinto 9:8-10)

**5** Lamulo la chikhalidwe liri ndi mphamvu pa anthu onse ku nthawi zonse, anthu [k]okhulupilira ndi ena onse, kuti akamvere lamuloli, osati chifukwa cha zomwe zikunenedwa mu lamuloli, komanso pa kulemekeza [l]ulamuliro wa Mulungu Namalenga, amene analipereka; Khristu mu Uthenga Wabwino samathetsa lamuloli konse koma [m]amalimbikitsa lamuloli.

([k]Aroma 13:8-10; Yakobo 2:8,10-12; [l]Yakobo 2:10-11;
[m]Mateyu 5:17-19; Aroma 3:31)

**6** Ngakhale anthu okhulupilira oonadi siali pansi pa chilamulo ngati chipangano cha zi ntchito, kuti [n]akalungamitsidwe nalo kapena kugamulidwa, komabe chilamulochi ndi chofunikira kwa iwo komanso anthu ena onse, chifukwa ndi chotitsogolera m'moyo, kuwauza iwo za chifuniro cha Mulungu ndi udindo wawo, chimawalondolera ndi kuwalamulira iwo kuti akathe kuyenda molingana ndi lamuloli, kuti pamene iwo [o]azindikira zovunda za makhalidwe ndi chilengedwe chawo, mitima ndi miyoyo yawo, atazifufuza iwo okha pogwiritsa ntchito chilamulochi, iwo akhoza kutsutsika za, kuchita manyazi ndi, komanso kudana ndi tchimo; pamodzi ndi kuonetsetsa bwino bwino kusowa kwawo kwa Khristu pa moyo wawo ndi kumvera kwawo kwa Iye; chimodzimodzinso anthu otembenuka mtima kuti akathe kuletsa zofooka zawo, pakuti lamuloli limakaniza tchimo; ndipo zoopseza zake zimaonetsera zomwe iwo akuyenera kulandira kamba ka machimo awo, ndi zovuta zomwe angayembekezera m'moyo uno chifukwa cha machimowo, ngakhale iwo anamasulidwa ku matembelero ndi mphamvu za lamuloli. Malonjezano a lamuloli amawawonetsa kubvomereza kwa

Mulungu pa kumvera kwawo ndi madalitso amene angawayembekezere pakumvera malamulowa, ngakhale sakuyenera kuchita izi ngati chipangano cha zintchito; koma monga munthu ayenera kuchita chabwino ndi kupewa zoipa, chifukwa lamulo limalimbikitsa chimodzicho ndi kuletsa chinacho, si umboni wokuti iye ali pansi pa [p]chilamulo osati pansi pa chisomo.

([n]Aroma 6:14; Agalatiya 2:16; Aroma 8:1; 10:4; [o]Aroma 3:20; 7:7; ndi ndime zotsatira; [p]Aroma 6:12-14; 1 Petro 3:8-13)

**7** Za kagwiritsidwe ntchito ka chilamulo zonse zatchulidwa [q]sizotsutsana ndi chisomo cha Uthenga Wabwino, koma zikubvomerezana nawo, Mzimu wa Khristu kugonjetsa ndi [r]kupereka kuthekera kwa chifuniro cha munthu kuti achite mwa nsangala zomwe chifuniro cha Mulungu, chobvumbulutsidwa mu chilamulo, chimafuna kuti munthuyo achite.

([q]Agalatiya 3:21; [r]Ezekieli 36:27)

## Mutu 20

# Za Uthenga wa Bwino, ndi za Mwezo wa Chisomo Chake

**1** Chipangano cha zintchito pamene chinaononongedwa chifukwa cha tchimo chinakhala chosapindulitsa ku moyo, Mulungu chinamkondweretsa kupereka lonjezo la Mwana wake Khristu, [a]mbeu ya mzimayi ngati njira yoitanira anthu osankhidwa ndikupatsa kwa iwo chikhulupiliro ndi kulapa; lonjezo ili, [b]Uthenga Wabwino womwe uli thunthu lake, linaonetseredwa, ndipo ndi wofunikira pa kutembenuka ndi chipulumutso cha anthu ochimwa.

([a]Genesis 3:15; [b]Chibvumbulutso 13:8).

**2** Lonjezo la Khristu ndi chikhulupiliro mwa Iye limaonetseredwa [c]m'mau a Mulungu okha basi; ngakhale chilengedwe kapena, njira zomwe Mulungu amasamalira anthu, [d]sizimaonetsa za Yesu kapena za chisomo chake, nthawi zambiri zimangonenera mwa chithunzithunzi chosaonekera bwinobwino, kuti anthu amene asowekera chibvumbulutso cha Iye kudzera mu lonjezano kapena Uthenga wabwino [e]akathe kupeza chikhulupiliro chopulumutsa kapena kulapa.

([c]Aroma 1:17; [d]Aroma 10:14-15,17; [e]Miyambo 29:18; Yesaya 25:7; 60:2-3)

**3** Chibvumbulutso cha Uthenga Wabwino kwa anthu ochimwa, chinachitidwa nthawi ndi malo osiyanasiyana, mophatikizana ndi

malonjezo ndi malamulo kuti anthu amene uthengawo wapatsiridwa akathe kumvera, ichi ndi chifuniro [f]chachikulu cha Mulungu ndi zomusangalatsa Iye; osasunthidwa ndi makhalidwe kapena kusintha kwa machitidwe a anthu, kapena chifukwa cha kuwala kobwera popanda Uthenga wabwino, kumene palibe munthu amene [g]anapanga kapena angapange; choncho mu zaka zonse, kulalikira kwa Uthenga Wabwino kunapatsidwa kwa anthu ndi maiko kuti ukafalitsidwe ndi kukonzedwa mosiyanasiyana, malingana ndi uphungu wa chifuniro cha Mulungu.

([f]Masalmo 147:20; Machitidwe 16:7; [g]Aroma 1:18-32)

**4** Ngakhale Uthenga Wabwino ndi njira yokhayo yowonetsera Khristu ndi chisomo chopulumutsa, ndipo ndi wokwanira kuchita choncho; komabe kuti anthu amene ali okufa mu uchimo akabadwenso mwatsopano, kutsitsimutsidwa kapena kukonzedwanso, ndi [h]ntchito ya Mzimu Woyera pa moyo wonse kuti pakakhale kupangidwanso mwa munthu moyo wa uzimu watsopano; womwe popanda iwo palibenso njira yomwe angathe [i]kutembenukira kwa Mulungu.

([h]Masalmo 110:3; 1 Akorinto 2:14; Aefeso 1:19-20;
[i]Yohane 6:44; 2 Akorinto 4:4,6)

## Mutu 21

# Za Ufulu wa Chikhristu ndi Ufulu wa Chikumbumtima

**1** Mu ufulu womwe Yesu anagulira anthu okhulupilira pansi pa Uthenga Wabwino, muli ufulu ku kutsutsika kamba ka tchimo, mkwiyo wa Mulungu, mphamvu ndi [a]matembelero a chilamulo, komanso kuomboledwa kwawo ku zoipa za [b]dziko lino, ku ukapolo wa [c]Satana, ndi ulamuliro wa [d]tchimo, ku [e]zosautsa zoipa, ku mantha a chigonjetso cha [f]imfa, chipambano cha kumanda ndi [g]chilango cha muyaya: chimodzimodzinso kwa iwo kwapatsidwa chilolezo [h]chaulere chopita pa maso pa Mulungu, komanso kumvera kwao kwa Iye, osati chifukwa cha mantha a ukapolo, koma ngati momwe [i]mwana amamvera atate ake mwa chikondi ndi mtima wosawiringula. Zonsezi zinali zodziwika ndi okhulupilira a pansi pa chilamulo pakuti chinali chinthu [k]chofunika kwa iwo; koma pansi pa chipangano chatsopano ufulu wa a Khristu wachulukitsidwa, mu ufulu wawo ku chilamulo cha miyambo, chomwe mpingo wa Ayuda unali kutsatira, ndiponso kuthekera kwa Akhristu kopita pa maso pa Mpando wa chisomo, komanso kulumikizana mwa

ulere ndi [l]Mzimu wa Mulungu, koposera okhulupilira a pansi pa chilamulo amachitira.

([a]Agalatiya 3:13; [b]Agalatiya 1:4; [c]Machitidwe 26:18; [d]Aroma 8:3; [e]Aroma 8:28; [f]1 Akorinto 15:54-57; [g]2 Atesalonika 1:10; [h]Aroma 8:15; [i]Luka 1:73-75; 1 Yohane 4:18; [k]Agalatiya 3:9,14; [l]Yohane 7:38-39; Ahebri 10:19-21)

**2** Mulungu yekha ndi [m]Ambuye wa chikumbumtima, ndipo sanachimange icho ku ziphunzitso ndi malamulo a anthu omwe ali [n]otsutsana ndi mawu ake, kapena osapezeka m'mawu ake. Choncho mwakuti kukhulupilira ziphunzitso zimenezi kapena kumvera izo mwa chikumbumtima ndi [o]kuphwanya ufulu wa icho, komanso kukakamiza anthu kuti akhale ndi chikhulupiliro chopanda [p]maonekedwe ake, kumvera chabe popanda zifukwa zenizeni, ndi kuononga ufulu wa chikumbumtima.

([m]Yakobo 4:12; Aroma 14:4; [n]Machitidwe 4:19,29; 1 Akorinto 7:23; Mateyu 15:9; [o]Akolose 2:20,22-23; [p]1 Akorinto 3:5; 2 Akorinto 1:24)

**3** Anthu amene amachimwa ponamizira ufulu wa Chikhristu, kapena kunyadilira chilakolako cha tchimo, akachita chonchi amalakwitsa chikonzero cha chisomo cha Uthenga Wabwino ku [q]chionongeko chawo chomwe, amaonongeratu [r]cholinga cha ufulu wa Chikhristu, womwe uli, kuti popeza talanditsidwa ku manja a adani athu onse, tikathe kutumikira Mulungu mopanda mantha, mopatulika ndi muchiyero pa maso pake, masiku onse a moyo wathu. (Aroma 6:1-2; Agalatiya 5:13; 2 Petro 2:18,21)

## Mutu 22

# Za Chipembezo ndi Tsiku la Sabata

**1** Kuwala kwa chilengedwe kumaonetsa kuti kuli Mulungu, yemwe ndi Mbuye ndipo ali ndi ulamuliro pa onse; Mulungu ndi wachilungamo, wabwino, ndipo amachita zabwino kwa onse; ndipo ayenera kupatsidwa ulemu, kukondedwa, kutamandidwa, kuitanira pa Iye, kukhulupilira mwa Iye, kutumikiridwa, ndi mtima wonse ndi moyo wonse [a]ndi mphamvu zonse. Koma njira yobvomerezeka yopembezera Mulungu yoona [b]anakhazikitsa Iye mwini, ndi kupatsidwa malire ndi chifuniro chake choonetseredwa, kuti Iye asakapembezedwe malingana ndi momwe maganizo ndi zipangizo zopangidwa ndi munthu, osatinso maganizo a Satana, pansi pa chionetsero chilichonse, kapena [c]njira iliyonse yomwe siinalembedwe M'mawu Opatulika.

([a]Yeremiya 10:7; Mariko 12:33; [b]Deuteronomo 12:32; [c]Eksodo 20:4-6)

**2** Chipembezo cha uzimu chikuyenera kupatsidwa kwa Mulungu Tate, Mwana ndi Mzimu Woyera, kwa Iye [d]yekha osati kwa angelo, anthu okhulupira, kapena [e]zolengedwa zina; ndipo chigwereni munthu, opanda mkhala [f]pakati, kapena mu kukhala pakati kwa wina koma[g] Yesu yekha.

([d]Mateyu 4:9-10; Yohane 4:23; Mateyu 28:19; [e]Aroma 1:25; Akolose 2:18; Chivumbulutso 19:10; [f]Yohane 14:6; [g]1 Timoteo 2:5)

**3** Kupemphera ndi kuthokoza zomwe zili zimodzi mwa chipembezo, Mulungu amafuna [h]anthu onse kuti azichita choncho. Koma kuti izi Mulungu akabvomereze, zikuyenera kuchitidwa mu [i]dzina la Mwana, mothandizidwa [k]ndi Mzimu Woyera molingana ndi [l]chifuniro chake, momvetsetsa, mwaulemu, modzichepetsa, mwamtima wonse ndi kupilira; pamene pali anthu ena mu [m]chinenero chodziwika.

([h]Masalmo 95:1-7; 65:2; [i]Yohane 14:13-14; [k]Aroma 8:26; [l]1 Yohane 5:14; [m]1 Akorinto 14:16-17)

**4** Pemphero likuyenera kunenedwa ku zinthu zoyenelera, ndi kwa anthu onse omwe ali moyo, [n]kapena kwa amene adzakhale m'tsogolo; [o]koma osati kwa anthu amene anamwalira, kapena amene angadziwike [p]kuti anapanga tchimo la ku imfa.

([n]1 Timoteo 2:1-2; 2 Samueli 7:29; [o]2 Samueli 12:21-23; [p]1 Yohane 5:16)

**5** [q]Kuwerenga Malemba, ulaliki ndi [r]kumva Mau a Mulungu, kuphunzitsa ndi kuchenjezana wina ndi mzake kudzera m'masalimo ndi nyimbo zoyamika [s]Mulungu ndi nyimbo za uzimu, kuimba ndi chisomo m'mitima yathu kwa Mulungu; komanso ngati mayendetsedwe [t]a ubatizo [u]ndi m'gonero wa Ambuye, zonsezi ndi gawo la kupembeza Mulungu, zoyenera kuchitidwa mwakumvera Iye ndi kumvetsetsa, mwa chikhulupiliro, mwa ulemu ndi moopa Mulungu, komanso, kudzichepetsa koona ndi [x]kutsara kudya, kuthokoza kwa nthawi [y]yapadera, zikuyenera kugwiritsidwa ntchito mu njira yopatulika ndi mwa umulungu.

([q]1 Timoteo 4:13; [r]2 Timoteo 4:2; Luka 8:18; [s]Akolose 3:16; Aefeso 5:19; [t]Mateyu 28:19-20; [u]1 Akorinto 11:26; [x]Estere 4:16; Yoweli 2:12; [y]Eksodo 15:1-19, Masalmo 107)

**6** Pemphero kapena kupembeza kulikonse komwe kuli pansi pa Uthenga Wabwino, si kuli kololedwa chifukwa cha malo omwe [z]zikuchitikira, kapena kuyang'ana; koma Mulungu akuyenera kupembezedwa paliponse mu uzimu ndi choonadi; ngati [a]m'mabanja pamodzi [b]tsiku ndi tsiku ndi malo a [c]chinsisi munthu payekha; motsindika pa kusonkhana pamodzi m'magulu opembeza, amene munthu sakuyenera [d]kunyozera, ndi

kusalabadiliridwa, pamene Mulungu kudzera m'Mau ake kapena mu njira zake anaitanira kusonkhanaku.

([z]Yohane 4:21; Malaki 1:11; 1 Timoteo 2:8; [a]Machitidwe 10:2; [b]Mateyu 6:11; Masalmo 55:17; [c]Mateyu 6:6; [d]Ahebri 10:25; Machitidwe 2:42)

**7** Ngati lamulo la chilengedwe, nyengo yokhazikika mwa chikonzero cha Mulungu, ikuyenera kupatulidwa padera malingana ndi Mau ake kuti ikakhale yopembedzera Mulungu mwa chilamulo cha chikhalidwe ndi lamulo lopitilira kulamulira anthu onse, ku mibadwo yonse, Mulungu anasankha tsiku limodzi mwa masiku asanu ndi awiri kukhala la [e]Sabata ndi kukhala lopatulika kwa Iye, lomwe kuyambira pa chiyambi cha dziko lino mpakana kuuka kwa Yesu Khristu linali tsiku lomaliza pa sabata, [f]ndipo kuyambira pa kuuka kwa Yesu linasinthidwa kupita pa tsiku loyamba la pa sabata lomwe limatchedwa Tsiku la Ambuye; ndipo likuyenera kupitilira mpakana kumathero a dziko ngati Sabata la Khristu; kuchita Sabata tsiku lomaliza pa sabata kunathetsedwa.

([e]Eksodo 20:8; [f]1 Akorinto 16:1-2; Machitidwe 20:7; Chivumbulutso 1:10)

**8** Choncho Sabata limasungidwa lopatulika kwa Mulungu, anthu pamene amaliza kukonzekeretsa mitima yawo, ndi kukonza zochita zawo tsikuli lisanafike, iwo samangomvera [g]za tsiku lonse la mpumulo wopatulika, ku zintchito zawo, mawu ndi maganizo komanso zintchito zawo zakudziko ndi zisangalalo komanso iwo amakhala nawo pamodzi ku nthawi ya msonkhano wa mapemphero ndi kupembeza kwa padera kwa munthu payekha, ndi zintchito [h]za chifundo ndi zoyenerera.

([g]Yesaya 58:13; Nehemiya 13:15-22; [h]Mateyu 12:1-13)

## Mutu 23

# Za Malumbiro Obvomerezeka ndi Kuwinda

**1** Lumbiro lobvomerezeka ndi mbali imodzi ya kupembeza, imene munthu [a]akamalumbira mwa chilungamo, mu chiyero, ndi chiweruziro, ndi kuitanira pa Mulungu kuti achitire umboni zomwe akulumbira iye, ndi kuti [b]amuweruze malingana ndi choonadi kapena bodza la lumbirolo.

([a]Eksodo 20:7; Deuteronomo 10:20; Yeremiya 4:2; [b]2 Mbiri 6:22-23)

**2** Pa dzina la Mulungu lokha ndi pomwe tiyenera kulumbira; ndipo likuyenera kugwiritsiridwa ntchito polumbira, moopa Mulungu ndi mwaulemu; choncho kulumbira wamba kapena mosalingalira

bwinobwino pa dzina looMasalmo ndi la ulemelero limenelo, kapena kulumbira pa chinthu china ndi tchimo, ndipo tiyenera [c]kunyasidwa nazo; komabe pa nthawi ya zinthu zofunikira, pofuna kutsimikizira choonadi, ndi [d]kuthetsa zitsutsano zonse, lumbiro limabvomerezeka ndi Mau a Mulungu; choncho lumbiro lobvomerezeka lomwe laikidwa ndi [e]ulamuliro wobvomerezeka mu zinthu monga zimenezi, likuyenera kutengedwa.

([c]Mateyu 5:34,37; Yakobo 5:12; [d]Ahebri 6:16,
2 Akorinto 1:23; [e]Nehemiya 13:25)

**3** Yense amene angapange lumbiro lobvomerezeka ndi Mawu a Mulungu, akuyenera kulingalira za kufunikira ndi kulemekezeka kwa mchitidwewu, ndipo mwa ilo kunena choonadi chokhachokha; chifukwa malumbiro ochitidwa mopanda kulingalira, abodza ndi opanda pake [f]amamukwiyitsa Mulungu, ndipo chifukwa cha ichi dziko limalira.

([f]Levitiko 19:12; Yeremiya 23:10)

**4** Malumbiro akuyenera kupangidwa momveka ndi [g]mawu amene akupereka nzeru, popanda kuzemba kapena maganizo obisika. ([g]Masalimo 24:4)

**5** Kuwinda, kumene kukuyenera kupangidwa kwa Mulungu yekha osati cholengedwa chilichonse, kukuyenera kupangidwa mwa [h]ulemu wa chipembedzo ndi mokhulupirika; koma kuwinda kwangati papa [i]kokhala moyo wa umbeta, kukhala mu [k]umphawi, ndi kumvera kwa kawirikawiri, sikuti munthu wafikapo pamwamba pa ungwiro wonse, ndipo ndi zikhulupiliro zosakhala za umulungu komanso [l]misampha ya uchimo, yomwe Mkhristu aliyense sakuyenera kupezekamo.

([h]Masalimo 76:11; Genesis 28:20-22; [i]1 Akorinto 7:2,9;
[k]Aefeso 4:28; [l]Mateyu 19:11)

## Mutu 24
# Za Udindo wa Boma

**1** Mulungu, Mbuye wa mkulu ndi Mfumu ya dziko lonse lapansi, anakonza kuti [a]maudindo a boma a m'maiko akhale pansi pa ukulu wake, ndipo anthu pansi pa boma, chifukwa cha ulemelero wake ndi ubwino wa anthu onse, chifukwa cha ichi Mulungu anapereka mphamvu ya lupanga, kuti akathe kuteteza ndi kulimbikitsa anthu kuti akachite zabwino, ndi kulanga anthu ochita zoipa. ([a]Aroma 13:1-4)

**2** Palibe kulakwika kulikonse kuti mKhristu akatenge udindo wa boma pamene iye waitanidwa kuti akagwire ntchito; pakulondolera zinthu m'bomamo makamaka kukhadzikitsa [b]chilungamo ndi mtendere malingana ndi malamulo a dziko lake, choncho chifukwa cha ichi akhonza pansi pa Chipangano Chatsopano [c]kulimbikitsa chilungamo pa zochitika zofunikira zonse. ([b]2 Samueli 23:3; Masalimo 82:3-4; [c]Luka 3:14)

**3** Mulungu pa kukhadzikitsa maudindo a boma pa zifukwa zomwe zanenedwa kalezi, kumvera zinthu zonse zobvomerezeka zolamuliridwa ndi boma kukuyenera kukhala udindo wathu ngati momwe tingamumvere Mulungu, osati chifukwa cha mkwiyo, [d]koma chifukwa cha chikumbumtima chathu; tikuyenera kupemphelera mafumu athu ndi onse amaudindo [e]kuti pansi pa ulamuliro wawo tikakhale moyo wamtendere mwa umulungu wonse ndi chilungamo.

([d]Aroma 13:5-7; 1 Petro 2:17; [e]1 Timoteo 2:1,2)

## Mutu 25

# Za Ukwati

**1** Ukwati ukuyenera kukhala pakati pa mwamuna m'modzi ndi mkazi m'modzi; [a]sizololedwa kuti mwamuna akhale ndi akazi opitilira m'modzi, kapena mkazi kukhala ndi amuna opitilira m'modzi.

([a]Genesis 2:24; Malaki 2:15; Mateyu 19:5-6)

**2** Ukwati unakonzedwa kuti [b]mwamuna ndi mkazi akathe kuthandizirana mofanana, kuti chiwerengero cha anthu pa dziko pano chichuluke mu njira yobvomerezeka, komanso ngati njira yoletsa chisembwere.

([b]Genesis 2:18; [c]Genesis 1:28; [d]1 Akorinto 7:2,9)

**3** Ndikololedwa kuti anthu [e]osiyanasiyana akathe kukwatirana, omwe angathe kupanga chisankho mwa nzeru; komabe ndi udindo wa mkhristu aliyense kuti [f]akwatire mwa Ambuye; choncho amene ali okhulupilira m'choonadi sakuyenera kukwatira anthu osakhulupira kapena [g]opembeza mafano, komanso anthu okhulupira Mulungu asakhale omangidwa m'goli ndi osakhulupilira, pokwatirana ndi anthu oipa m'moyo wawo, kapena anthu opatukira m'chiphunzitso.

([e]Ahebri 13:4; 1 Timoteo 4:3; [f]1 Akorinto 7:39; [g]Nehemiya 13:25-27)

**4** Ukwati sukuyenera kuchitika pakati pa anthu a banja [h]limodzi kapena pachibale, moletsedwa ndi Mawu a Mulungu; komanso maukwati amenewa sakuyenera kulolezedwa ndi malamulo a dziko lirilonse, kapena

ngakhale anthu awiri [i]atagwirizana kukhalira pamodzi.

([h]Levitiko 18; [i]Mariko 6:18; 1 Akorinto 5:1)

# Mutu 26
# Za Mpingo

**1** Mpingo wa dziko lonse (womwe Mzimu woyera ndi choonadi cha chisomo chimagwira ntchito mkati mwake) umatha kutchedwa mpingo wosaoneka, womwe umakhala ndi anthu [a]onse osankhidwa, omwe anakhala, omwe ali, ndi amene adzasonkhanitsidwe pamodzi mwa Yesu, yemwe ali Mutu wa Mpingo, ndipo ndi mwamuna wa thupi, thunthu la iye amene akwana mwa onse.

([a]Ahebri 12:23; Akolose 1:18; Aefeso 1:10,22-23; 5:23,27,32)

**2** Anthu onse pa dziko lapansi, omwe amanena za chikhulupiliro mwa Uthenga Wabwino, ndi kumvera Mulungu kudzera mwa Yesu malingana ndi Uthenga wabwinowo, osaononga chikhulupiliro chawo ndi zolakwika zosokoneza maziko, kapena kusapatulika kwa mayankhulidwe, [b]ali ndipo akhonza kutchedwa anthu a Mulungu ooneka; [c]ndipo mipingo yonse iyenera kukhala nawo.

([b]1 Akorinto 1:2; Machitidwe 11:26; [c]Aroma 1:7; Aefeso 1:20-22)

**3** Mipingo yabwino yomwe ili pa dziko lapansi imakhala ndi kuthekera kokhala [d]ndi kasakaniza ndi zolakwika, ndipo mipingo ina inatailira [e]ndi kusakhalanso ngati mipingo ya Khristu, koma mipingo ya Satana; ngakhale zili chonchi Khristu Yesu nthawi zonse anakhala ndipo adzakhala ndi ufumu mdziko muno, mpakana kumathero, kwa onse amene akhulupira mwa Iye ndikunenera dzina Lake.

([d]1 Akorinto 5; Chivumbulutso 2-3; [e]Chivumbulutso 18:2; 2 Atesalonika 2:11-12; [f]Mateyu 16:18; Masalmo 72:17; 102:28; Chivumbulutso 12:17)

**4** Ambuye Yesu Khristu ndi Mutu wa Mpingo, amene, mwakusankha kwa Mulungu Atate, wapatsidwa [g]mphamvu zonse zoitanira, kukhadzikitsa, ndondomeko ndi kayendetsedwe ka mpingo, mu ukulu ndi ulamuliro pamwamba pa onse; mokuti Papa wa mpingo wa chikatolika wa ku Roma sangathe kukhala wotsogolera mpingo wa Yesu, koma ndi [h]iye yemwe ali wokana Khristu, ndi munthu wa uchimo, ndi munthu wolengedwera chilango, amene amadzikweza yekha mu Mpingo mokana Yesu ndi zonse zimene zimatchedwa za Mulungu; amene Mulungu adzamuononge ndi kuwala kwa kubwera kwake.

([g]Akolose 1:18; Mateyu 28:18-20; Aefeso 4:11-12; [h]2 Atesalonika 2:2-9)

**5** Pakugwiritsa ntchito mphamvu zomwe zinapatsidwa kwa Iye, Ambuye Yesu amaitanira anthu kuchokera ku dziko kwa Iye yekha, kudzera mu utumiki wa Mau ake, ndi Mzimu wake, [i]onse amene apatsidwa kwa Iye ndi Atate kuti akayende pa maso pake mu [k]njira zonse za kumvera, zomwe analemba m'mawu ake. Choncho onse oitanidwa, anawalamula kuti akayende pamodzi, m'magulu awo awo, kapena [l]m'mipingo yawo kuti akathe kulimbikitsana ndi mchitidwe wa kupembeza pamodzi, womwe Iye amawalumulira iwo kuti akachite pa dziko pano.

([i]Yohane 10:16; [k]Yohane 12:32; Mateyu 28:20; [l]Mateyu 18:15-20)

**6** Mamembala a mipingo imeneyi ndi [m]anthu oyitanidwa a Mulungu, amaonetsera ndi kupereka umboni (m'mayendedwe awo ndi kubvomereza kwao) mu kumvera kwao zonse zimene zili za Khristu; ndi mwakufuna kuchita kuyenda pamodzi, malingana ndi momwe Khristu wasankhira; kudzipereka okha kwa Ambuye, ndi kwa wina ndi mzake mwa chifuniro cha Mulungu, [n]mobvomereza kumvera malamulo a Uthenga Wabwino.

([m]Aroma 1:7; 1 Akorinto 1:2; [n]Machitidwe 2:41-42; 5:13-14; 2 Akor. 9:13)

**7** Kwa mipingo yonse payokha payokha yosonkhana, molingana ndi malingaliro ake olembedwa M'mau ake, anapereka [o]ulamuliro ndi mphamvu zonse, zomwe zili zofunika mu njira zonse kuti akachite moyenerera pa kupembeza, makhalidwe, omwe anawaikira iwo kuti akamvetsere; ndi malamulo oyenera okuti akagwiritse ntchito mphamvuzo. ([o]Mateyu 18:17,18; 1 Akorinto 5:4,5; 5:13; 2 Akorinto 2:6-8)

**8** Mpingo pawokha, wosonkhana ndi wokonzedwa malingana ndi maganizo a Khristu, umakhala ndi ogwira ntchito ndi mamembala; ndi ogwira ntchito osankhidwa ndi Khristu akuyenera kusankhidwa ndi kupatulidwa ndi Mpingo (oitanidwa ndi kusonkhanitsidwa), kuti akathe kugwira ntchito kuchita malamulo, ndi kugwiritsa mphamvu za udindo, womwe Khristu anawapatsira iwo, kapena kuwaitanira iwo, mpakana kumathero a dziko lino ndi [p]akulu a mpingo, ndi atumiki.

([p]Machitidwe 20:17,28; Afilipi 1:1)

**9** Njira yomwe Khristu anakhadzikitsa yoitanira anthu, opatsidwa mphatso ndi Mzimu Woyera kuti akakhale akulu ampingo mu mpingo, ndi yokuti [q]akasankhidwe molingana ndi mgwirizano wa mpingo wonse; komanso kupatulidwa padera ndi kutsala kudya ndi pemphero ndi kusanjikidwa manja ndi [r]akulu akulu ena a mumpingo amene anakhala alipo kuyambira kale; ndiponso anthu otumikira [s]akuyenera kusankhidwanso chimodzimodzi, ndi kupatulidwa ndi pepemphero ndi kusanjikidwa manja.

([q]Machitidwe 14:23; [r]1 Timoteo 4:14; [s]Machitidwe 6:3,5-6)

**10** Ntchito ya azibusa ndi yotumikira Khristu mu Mipingo Yake, mu utumiki wa Mawu ndi mapemphero [t]ndi kuyang'anira miyoyo yawo pakuti akuyenera kudzayankha kwa Mulungu; ndi udindo wa mipingo yomwe amatumikira kuti idziwapatsa ulemu wonse, [u]komanso kuwagawira iwo zinthu zabwino malingana ndi kuthekera kwao, choncho kuti iwo azitha kukhala ndi zinthu mosavuta, popanda iwo [x]kutangwanika ndi zinthu za kudziko, komanso kuti athenso [y]kusamalira ndi kulandira anthu ena; monga m'mene [z]lamulo la chikhalidwe limanenera komanso chifukwa cha lamulo la Yesu Khristu amene analamulira kuti amene akulalikira Uthenga Wabwino akuyenera kukhala m'mawu ake.

([t]Machitidwe 6:4; Ahebri 13:17; [u]1 Timoteo 5:17-18; Agalatiya 6:6-7; [x]2 Timoteo 2:4; [y]1 Timoteo 3:2; [z]1 Akorinto 9:6-14)

**11** Ngakhale uli udindo wa mabishop kapena azibusa a m'mipingo, kuti azikakhala amachawi pa kulalikira mawu a Mulungu, molingana ndi udindo wawo, komano ntchito yolalikira siili ya iwo okha, komanso anthu ena amene, ali ndi [a]mphatso yopatsidwa ndi Mzimu Woyera kuti akathe kuchita choncho, mobvomerezedwa ndi kuitanidwa ndi mpingo akhoza kulalikira.

([a]Machitidwe 11:19-21; 1 Petro 4:10-11)

**12** Anthu okhulupilira akuyenera kukhala mu mpingo, kumene ndi pamene iwo angathe kuchita chomwecho, ndi cholinga chokuti akathe kutenga gawo pa zinthu zochitika mu mpingo, komanso akuyenera kukhala [b]pansi pa ulamuliro wake, malingana ndi momwe Khristu analamulira.

([b]1 Atesalonika 5:14; 2 Atesalonika 3:6,14-15)

**13** Pasakhale membala aliyense wa mpingo, amene walakwira ndipo mpingo watsatira ndondomeko yonse yokhudzana munthu wolakwirayo, sakuyenera kusokoneza bata mumpingomo, kapena kuleka kubwera ku misonkhano ya mpingo, kapena ku ulamuliro wa mpingo chifukwa cha mlandu umene wachitidwa kwa membala nzawo wa mu mpingomo, koma akuyenera kudikilira pa Khristu, [c]momwe mpingowo ungachitire nayo nkhaniyo.

([c]Mateyu 18:15-17; Aefeso 4:2-3)

**14** Pakuti mpingo uliwonse ndi mamembala a m'mipingo yonse akulamulilidwa kuti akuyenera [d]kupempherera ubwino ndi kupita patsogolo kwa mipingo yonse ya Khristu pa dziko lapansi, ndi munthawi zonse aliyense payekha m'malo omwe amakhala ndi maitanidwe awo

kugwiritsa ntchito mphatso ndi zisomo zawo, pamene mipingo mwa chisomo ndi chikonzero cha Mulungu, ingadzalidwe, pamene ikathe kupindula nawo, iyenera kukhala mwa [e]chimvano mwa iyo yokha, ku mtendere wawo, kukulitsa kwa chikondi, ndi kulimbikitsana wina ndi unzake.

([d]Aefeso 6:18; Masalmo 122:6; [e]Aroma 16:1-2; 3 Yohane 8-10)

**15** Pamene pali zovuta kapena kusagwirizana, pa nkhani ya kayendetsedwe ka zinthu kapena ziphunzitso, pamene mipingo pamodzi ili yokhudzidwa kapena mpingo umodzi, mu mtendere wawo, kugwirizana kwawo ndi chilimbikitso; kapena membala m'modzi kapena mamembala angapo a mpingo wina wake apwetekeka, kapena mu zotsatira za chidzudzulo sali kugwirizana ndi choonadi ndi bata; ndi molingana ndi Mau a Khristu, kuti mipingo yomwe imagwirizana pamodzi, kudzera mwa atumwi awo, kukumana ndi kulingalira, [f]ndi kupereka malangizo okhudzana ndi zinthu zomwe ali kusiyana maganizo, ndi tsatanetsatane wake kuperekedwa kwa mipingo yomwe ili yokhudzidwa, chikhalire icho, atumwi osonkhanawa sapatsidwa mphamvu zili zonse za kumpingo, kapena ulamuliro uliwonse pa mipingo, kapenanso kudzudzula mipingo kapena anthu a m'mpingoyi, komanso [g]kupereka maganizo awo kwa anthu oyang'anira mipingoyi.

([f]Machitidwe 15:2,4,6,22-23,25; [g]2 Akorinto 1:24; 1 Yohane 4:1)

## Mutu 27

# Za Chiyanjano cha Okhulupilira

**1** Anthu onse okhulupilira ali oyanjanitsidwa kwa Yesu Khristu, mutu wawo, kudzera mwa Mzimu wake ndi chikhulupiliro, ngakhale iwo samapangidwa kukhala munthu m'modzi ndi Iye, amakhala ndi [a]chiyanjano mu zisomo zake, mazunzo ake, imfa yake, kuuka, ndi ulemelero wake; pokhalanso olunzanitsidwa wina ndi mzake mu chikondi, amakhala mu [b]chiyanjano cha mphatso ndi zisomo za wina ndi mzake ndipo akuyenera kuchita ntchito zimenezi, pabwalo komanso mwachinsisi, mwadongosolo, kuti zikam'chitire [c]ubwino aliyense, mkati mwawo ndi kunja komwe.

([a]1 Yohane 1:3; Yohane 1:16; Afilipi 3:10; Aroma 6:5-6; [b]Aefeso 4:15-16; 1 Akorinto 12:7; 3:21-23; 1 [c]Atesalonika 5:11,14; Aroma 1:12; 1 Yohane 3:17-18; Agalatiya 6:10)

**2** Anthu okhulupilira akuyenera kukhala mu chiyanjano chopatulika mu kupembeza Mulungu, ndi kuchita ntchito zina za uzimu kuti [d]akalimbikitsane wina ndi mzake; ndi kuthandizana kuchita ntchito zina ndi zina malingana ndi kuthekera kwao, ndi kufunikira kwa ntchitozo; chiyanjanochi, malingana ndi malamulo a Uthenga Wabwino, ngakhale kuti chiyenera kuchitidwa ndi iwo mokhudzana ndi komwe iwo ali, monga [f]m'mabanja awo kapena [g]m'mipingo, koma malingana ndi kuthekera komwe Mulungu angapereke, chikuyeneranso kuchitira izi kwa anthu onse okhulupilira, kwa onse amene amaitanira pa dzina la Ambuye Yesu; ngakhale zili chonchi, chiyanjano chawo ngati anthu oyera mtima, sichitanthauza kuti palibe yemwe angakhale ndi umwini pa zinthu ndi katundu.

([d]Ahebri 10:24-25; 3:12-13; [e]Machitidwe 11:29-30; [f]Aefeso 6:4; [g]1 Akorinto 12:14-27; [h]Machitidwe 5:4; Aefeso 4:28).

## Mutu 28
# Za Ubatizo ndi Mgonero wa Ambuye

**1** Ubatizo ndi mgonero wa Ambuye ndi lamulo, lokhazikitsidwa ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye Yesu, yekhayo wopereka lamulo, kuti likachitidwe [a]mpakana kumathero a dziko lino.

([a]Mateyu 28:19-20; 1 Akorinto 11:26)

**2** Malamulo awiriwa akuyenera kuchitidwa ndi anthu obvomerezeka, oitanidwa kuti akathe kuchita chomwechi, molingana [b]ndi momwe Khristu analamulira. ([b]Mateyu 28:19; 1 Akorinto 4:1)

## Mutu 29
# Za Ubatizo

**1** Ubatizo ndi choikika cha mu Chipangano Chatsopano, chimene Yesu Khristu anaika, kuti chikhale kwa iye wobatizidwa, ngati chizindikiro cha chiyanjano chake ndi Yesu, mu imfa yake, ndi [a]kuukanso kwake kwa akufa; kumezanitsidwa mwa Iye, [b]kuchotsedwera machimo; ndi kugonjera kwa Mulungu kudzera mwa Yesu Khristu, kuti [c]akayende mu moyo wa tsopano.

([a]Aroma 6:3-5; Akolose 2:12; Agalatiya 3:27; [b]Mariko 1:4; Machitidwe 22:16; [c]Aroma 6:4)

**2** Amene amaonetsera kuti ndi [d]otembenuka mtima kwa Mulungu, okhulupilira, ndi omvera Ambuye wathu Yesu, ndi okhawo amene ali oyenera kulandira choikikachi.

([d]Mariko 16:16; Machitidwe 8:36-37; 2:41; 8:12; 18:8)

**3** Chipangizo chogwiritsira ntchito pokwaniritsa choikikachi ndi [e]madzi, momwe munthu akuyenera kubatizidwa mu dzina la Atate, la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.

([e]Mateyu 28:19-20; Machitidwe 8:38)

**4** Kumiza, kapena kubviika [f]m'madzi munthu, ndiyo njira yoyenera pakukwaniritsa choikikachi.

([f]Mateyu 3:16; Yohane 3:23)

## Mutu 30

# Za Mgonero wa Ambuye

**1** Mgonero wa Ambuye unakhadzikitsidwa ndi Yesu mwini usiku umene anapachikidwa, kuti ukakhale ukuchitidwa mu mpingo wake mpakana kumathelo a dziko lino, kuti chikakhale chikumbutso, ndi chionetsero cha nsembe ya iye yekha mu imfa yake, [a]chitsimikizo cha chikhulupiliro cha anthu okhulupilira mu zopindulitsa zonse zomwe zilimo, chisamaliro cha moyo wawo wa uzimu, ndi kukula kwawo mwa Iye, ndi kudzipereka kwawo mu ntchito zonse zomwe ayenera kumuchitira Iye; [b]ndi kukhala choluzanitsa ndi kuzipereka ku chiyanjano ndi Iye komanso, munthu wina ndi mzake.

([a]1 Akorinto 11:23-26; [b]1 Akorinto 10:16-17,21)

**2** Mu chilamulo ichi, Khristu samaperekedwa kwa Atate ake, kapena nsembe yeniyeni simakhala ikuchitika, kutsuka machimo a anthu amoyo ndi akufa, koma ndi chikumbutsiro chakudzipereka yekha kwake pa mtanda, [c]kamodzi kwa nthawi zonse; ndi chopereka cha [d]chipembezo chopereka matamando kwa Mulungu. Kotero misa ya akatolika yomwe imatchedwa nsembe ndi chinthu chodetsedwa, ndi chochotsa ulemu nsembe ya Yesu, yokhayo yomwe ndi imene imalipilira machimo a anthu onse osankhidwa pa dziko lapansi.

([c]Ahebri 9:25-26,28; [d]1 Akorinto 11:24; Mateyu 26:26-27)

**3** Ambuye Yesu Khristu mu chilamulo ichi, anasankha omutumikira kuti akapemphere, ndi kudalitsa zida za Mkate ndi Vinyo ndi kuti zikakhale zopatulika ku ntchito za chisawawa ndikuti zikagwire ntchito yopatulika,

ndi kutenga ndi kudya mkate; ndi kutenga chikho, [e]komanso kuwagawira anthu omwe akuwatumikira.

([e]1 Akorinto 11:23-26)

**4** Kuletsa anthu ena kumwa chikho, kulambira zida, kuzikweza m'wamba, ndi kuzinyamula kuyendayenda nazo kuti zitamandidwe, ndi kuzisunga izo chifukwa cha mapembezo ena aliwonse, [f]zonsezi zikutsutsana ndi makhalidwe ndi momwe Yesu anakhadzikitsira.

([f]Mateyu 26:26-28; 15:9; Eksodo 20:4-5)

**5** Zida za chizindikiro za chilamulo, ndi zopatulidwa pambali kuti zikagwire ntchito yomwe Khristu anazikonzera, zili ndi ubale ndi kupachikidwa kwake, ngati zoona, ngakhale zili mongofananiza chabe, ngakhale zimatchulidwa maina a zinthu zomwe zikuimilira, [g]thupi ndi mwazi wa Khristu, mu chikhalidwe chawo, zimakhalabe [h]mkate ndi vinyo ngati momwe zinaliri kuyambira nthawi ya kale.

([g]1 Akorinto 11:27; [h]1 Akorinto 11:26,28)

**6** Chiphunzitso chomwe chimasintha zida monga mkate ndi vinyo kukhala ngati izo ndilo thupi ndi mwazi wa Yesu zotchedwa "transubstantiation" (chiphunzitso chomwe chimati thupi and mwazi zisanthulika zenizeni pamene mbusa wayala manja), pomwe wansembe amadzoza kapena mwa njira ina iliyonse, ndi zopanda pake pa maso a [i]Mawu a Mulungu komanso ku malingaliro a munthu, ndipo zimachotsa [k]tanthauzo la chilamulochi, ndipo zakhala, ndipo zili, chiyambi cha zikhulupiliro cha matsenga ndi zifano zosiyanasiyana.

([i]Machitidwe 3:21; Luka 24:6,39; [k]1 Akorinto 11:24-25)

**7** Anthu oyenera kulandira, pakutenga nawo gawo poyera pa zizindikiro zooneka mu chilamulochi, iwonso mkati mwawo mwa chikhulupiliro, osati ku thupi ndi mu chigulu, koma mwa uzimu amalandira, ndi kudya za Yesu wopachikidwa, [l]ndi zopindulitsa zonse za imfa yake; thupi ndi mwazi wa Khristu mwa uzimu kuperekedwa kwa chikhulupiliro cha anthu okhulupilira mu chilamulochi.

([l]1 Akorinto 10:16; 11:23-26)

**8** Anthu onse osadziwa ndi osakhulupilira, amene ali osathekera kukhala mu chiyanjano [m]ndi Khristu, iwowa sali ololedwa kudya mgonero wa Ambuye, anthuwa ngati adakalibe mu uchimo [n]sangayitanidwe kuti athe kudya nawo, inde, yense amene adzalandire mosayenera ali olakwa ku thupi ndi mwazi wa Ambuye, kudya ndi kumwa chiweruzo kwa iwo eni.

([m]2 Akorinto 6:14-15; [n]1 Akorinto 11:29; Mateyu 7:6)

# Mutu 31
# Za Kukhala kwa Munthu Akamwalira ndi Kuuka kwa Anthu Akufa

**1** Anthu akafa matupi awo amabwerera ku dothi, [a]ndi kuona chibvundi; koma mizimu yawo, yomwe siifa kapena kugona, yokhala ndi chikhalidwe cha muyaya, [b]imabwerera kwa Mulungu yemwe anaipatsa kwa iwo. Mizimu ya anthu oyera imapangidwa kukhala ya ngwiro mopatulika ndi kulandiridwa ku paradaiso, komwe ali ndi Yesu, ndi kuona nkhope ya Mulungu mu kuwala [c]ndi mu ulemelero, kuyembekezera chiwombolo cha matupi awo; ndipo mizimu ya anthu ochimwa imakanthidwira ku ng'anjo ya moto; komwe amakhala mu mazunzo ndi ku mdima wosatha, kusungidwira ku [d]chiweruzo cha tsiku lalikulu; kupatula malo awiriwa, palibenso malo ena omwe Mau a Mulungu amanena kuti munthu akafa amapita.

([a]Genesis 3:19; Machitidwe 13:36; [b]Mlaliki 12:7; [c]Luka 23:43; 2 Akorinto 5:1,6,8; Afilipi 1:23; Ahebri 12:3; [d]Yuda 6-7; 1 Petro 3:19; Luka 16:23-24)

**2** Pa tsiku lomaliza, anthu okhulupilira omwe adzakhala ali moyo, sadzagona ayi koma [e]adzasanthulika; ndipo onse akufa adzaukitsidwa ndi matupi awo anali nawo, [f]osati ena, koma adzakhala a [g]mtundu wina, amene adzayanjanitsidwe ndi mizimu yawo kwa muyaya.

([e]1 Akorinto 15:51-52; 1 Atesalonika 4:17; [f]Yobu 19:26-27; [g]1 Akorinto 15:42-43)

**3** Matupi a anthu osalungama, adzaukitsidwa ku chionongeko ndi mphamvu ya Khristu; matupi a anthu olungama adzaukitsidwa ndi Mzimu wake ku ulemelero, [h]ndi kupangidwa ofanana ndi thupi lake la ulemelero.

([h]Machitidwe 24:15; Yohane 5:28-29; Afilipi 3:21)

# Mutu 32
# Za Chiweruzo Chomaliza

**1** Mulungu anasankha tsiku lomwe adzaweruze dziko lino mwa chilungamo, [a]kudzera mwa Yesu Khristu; kwa Yemwe mphamvu ndi chiweruzo zinapatsidwa ndi Atate; tsiku lomwe [b]angelo opandukira ndi

anthu onse omwe anakhala pa dziko lapansi adzaonekere pa maso pa Khristu, [c]kudzayankha za maganizo, mawu, ndi zintchito zawo ndi kudzalandira malingana ndi zomwe anachita ku thupi, zabwino kapena zoipa.

([a]Machitidwe 17:31; Yohane 5:22,27; [b]1 Akorinto 6:3; Yuda 6; [c]2 Akorinto 5:10; Mlaliki 12:14; Mateyu 12:36; Aroma 14:10,12; Mateyu 25:32-46)

**2** Cholinga chomwe Mulungu anasankhira tsikuli, ndi chokuti, Mulungu akaonetsere ulemelero wa chifundo chake, mu chipulumutso cha anthu osankhidwa, [d]ndi za chilungamo chake, mu chionongeko cha anthu osakhulupilira, omwe ali ochimwa ndi akusamvera; pamene anthu olungama adzakalowe ku moyo wosatha, ndi kukalandira chimwemwe ndi ulemelero wodzadza ndi mphoto za muyaya, pa maso [e]pa Ambuye; koma anthu ochimwa, osadziwa Mulungu, osamvera Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, adzatayidwa pa mbali ku mazunzo osatha, ndi [f]kulangidwa ndi chionongeko chosatha, pa maso pa Ambuye ndi ku ulemelero wa mphamvu zake.

([d]Aroma 9:22-23; [e]Mateyu 25:21,34; 2 Timoteo 4:8; [f]Mateyu 25:46; Mariko 9:48; 2 Atesalonika 1:7-10)

**3** Pamene Khristu, akadakonda tonse titakhale okopeka mu mtima kuti kudzakhala tsiku la chiweruzo, [g]kuti akaletse anthu ochimwa ku uchimo wawo, ndi kuti chikakhala [h]chitonthozo kwa onse okhulupilira ku mazunzo awo, kuti tsikuli likadziwike kwa anthu onse, kuti iwo asakadalire chitetezo chosakhala cha Mulungu, ndi kukhala atcheru nthawi zonse, chifukwa sadziwa tsiku lomwe [i]Ambuye adzabwere, ndi kukakhala okonzeka kunena kuti "[k]Bwerani Ambuye Yesu; Bwerani msanga. Amen."

([g]2 Akorinto 5:10-11; [h]2 Atesalonika 1:5-7; [i]Mariko 13:35-37; Luka 12:35-40; [k]Chivumbulutso 22:20)